


CHIWOBOLO

KUKHALA CHOTSIRIZIKA,

MU CHISANGALALO

 Ndine wokondwa usikuuno, kachiwiri, kuti ndikupatseni inu moni mu Dzina la Ambuye wathu Yesu wokondedwa, Mwana woukitsidwa wa Mulungu. Ndipo Kukhalapo Kwake kunali kuli kale muno pamene ine ndimalowa, chotero ife tikuyembekezera kuti tiwone zochuluka, zoposa, “pamwamba pa zonse zimene tikhoza kuchita kapena kuziganizira,” usikuuno, kuti Mulungu atsanulira pa ife, a madalitso Ake, ndi kumukuza Yesu Khristu pakati pathu.

² Ine ndakhala ndikuyankhula mausiku awiri apitawa... Lamlungu usiku ine ndikuganiza ife tinali ndi msonkhano wa machiritso, ndipo Lolemba usiku ine ndimalalikira. Ndi kupereka... Ndinayamba phunziro, Lamlungu mmawa, mu kachisi. Ndipo ine ndinaganiza, pamene ife tinali kuyembekezera kuti gulu likhale ngati lanyamulidwa pang’ono, ine ndimakhala ngati ndimapereka mpata ku kumverera kwanga. Ndine...

³ Limodzi la masiku awa, Mulungu akalola, ndipo akandithandiza ine, ndikungofuna kuti ndidzakhale ndi misonkhano ingapo kumene inu—inu simutero... kungolowa ndi kukalalikira kapena kuphunzitsa Lemba, ndi kuitanira paguwa, ndi kutsikira pa guwa ndi kumawapempherera anthu, ndipo monga ife Abaptisti akachitidwe-kachikale tinkachitira. [Winawake akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Abaptisti awiri okha amene ndawamva akunena, “Ameni.” Chotero inu nonse muli kuti, usikuuno?

Winawake anati, “M’bale Branham, kodi inu munali wa Baptisti?”

Ndinati, “Eya,” ine ndinatero.

⁴ Ine ndinkalalikira kuno ku Arkansas, nthawi ina. Munthu, munthu wokalamba, anachiritsidwa. Iye anali... iwo anali... Iye anali wa Nazareni. Iye anali atanyamula ndodo zake pa nsana wake, tsiku lotsatiralo, akupita mozungulira mzinda, ali ndi—chikwangwani pa izo, “Mulungu wandichotsera ine izi, usiku wathawu.” Ndipo iye anali wolumala kwambiri. Kunali mu Little Rock. Ndipo iye anakhala ali chomwecho kwa zaka zingapo. Ndipo aliyense ankamudziwa iye, chifukwa ankayendayenda, ndipo amakhala ali ndi chipewa chake chiri

pansi, ndipo akugulitsa mapensulo kuchokera mchipewacho. Ndipo aliyense ankamudziwa iye, chotero izo zinangoyamba, zinangochita chinthu chachikulu mu mzindawo.

⁵ Ndipo mausiku angapo zitachitika zimenezo, ine ndimalalikira, ndipo—ndipo iye anadzuka. Iye anati, “Miniti yokha, M'bale Branham, kodi inu mungasamale ngati ine nditakufunsani inu chinachake?”

Ine ndinati, “Ayi, bwana.”

⁶ Ndipo iye anati, “Chabwino,” iye anati, “pamene—pamene ine ndinakumvani inu mukulalikira, ndinadziwa kuti ndinu wa Nazareni.” Iye anati, “Kenako ine ndinawawona anthu onse Achipentekoste ozungulira kuno, ndipo winawake anandiuza ine kuti inu ndi wa Pentekoste.” Iye anati, “Ine ndinakumvani inu mukuti, kanthawi kapitako, inu munali wa Baptisti.” Iye anati, “Sindikumvetsa zimenezi.”

⁷ Ine ndinati, “Chabwino, izo ndizophweka. Ndine wa Pentekoste Nazareni Baptisti.” Uko nkulondola. Uko nkulondola. Ndife basi . . . kukhulupirira.

⁸ Oh, amzanga, ine sindiri wa chipembedzo chirichonse cha mpingo, ndipo komabe ine ndi wa chirichonse cha iwo. Pamene ine ndimayamba pa izi, ine ndinati, “Khristu ndiye mutu wanga. Baibulo ili ndi bukhu langa lophunzirira. Ndipo dziko ndi mpingo wanga.” Chotero, izo—izo ndi zimene ine ndikufuna kuti ndikhale kufikirira ine nditafa.

⁹ Tsopano, mu usiku kapena uwiri, ife tidzayesa kuti tiyambitse msonkhano wa machiritso kachiwiri, pamene ife tidzapeza . . . Ndithudi, powona zonyamulira izi ndi machira ziri pozungulira panazi, ine ndikufuna kuti ndiwone chinachake. Ndine wofunitsitsa kufuna chinachake chitachitika kuno mu Louisville, Kentucky, chifukwa kuno ndi dera langa.

¹⁰ Ine sindinakhalepo ndi wabwino, umene inu mumawutcha msonkhano wabwino, mu Kentucky. Ndipo ine sindikutanthauza zimenezo ndi kuyipitsa kulikonse. Ine—ine ndakhalapo ndi oyipa kwambiri, malo ambiri. Koma, ine ndikutanthauza, komwe kuno kwathu komwe, izo ndizovuta kwambiri. Ine . . . basi zimavuta kwambiri kuti uziswe izo. Sindikudziwa chifukwa chake. Koma ine ndikuganiza ndi chifukwa chakuti Yesu anati, “Mdziko lako lomwe,” ndi momwe zingakhalire, ndizo mwinamwake—momwe zikukhalira. Koma sitimafika powona nkomwe zozizwitsa zopambana zambiri.

¹¹ Ine ndinali ndi msonkhano kuno, pafupifupi chaka kapena ziwiri zapitazo, mu Jeffersonville, koma zinachitika kuti mkaziyo anali wochokera kuno ku Kentucky kwina kwake. Iye anali atasanduka ngati choko, monga, kuyambira mmiyendo yake kumatsika; kuyambira mchiuno mwake mpaka ku miyendo yake, kani. Ndipo iye—iye anali asanayende, kwa zaka seventini. Ambiri a inu munali kumeneko usiku umenewo, ndipo

mukuikumbukira nkhaniyo. Ndipo iye anadzuka pomwepo ndipo anayenda akutuluka mkachisi, mwabwinobwino.

¹² Tsopano, ndikufuna kuti chinachake chiyambe kuno ku Louisville, kumene ine ndingathe kuwona chitsitsimutso cha kachitidwe-kachikale chikusesa mu mzinda wokondeka waukulu uno kuno.

¹³ Iwo ndi mzinda wonga mizinda ina yonse; iwo ndi woyipa monga yonse imatulukira. Inu mukudziwa izo ndi zoon. Ine sindikumupweteka Kentucky; chifukwa, ndine waku Kentucky, nanenso. Chabwino. Koma ndi—ndi zoon. Ndi woipa. Kuno ndi kwawo kwa kachasu yense ndi opanga kachasu, ndi zida zoyipa ndi chirichonse, chomwecho, izo zimachitika kozungulira Louisville, Kentucky kuno, kotero kuno ndi mpando wa Satana.

¹⁴ Koma ife tikhoza kuwuphwanya iwo mzidutswa ndi Uthenga wa Yesu Khristu, ngati ife tonse tingakhale pamodzi. Uko nkulondola. Ife tikuyenera kulumikizana mphamvu zathu pamodzi ndi kumakankha.

¹⁵ Nthawi yina yapitayo, mlaliki wotchuka kwambiri mu dziko anali, anati, akukamba za misonkhano kuno. Iye anati, “Chabwino, apa ndi chimene icho chiri.” Iye anati, “Ndikamapita mu mzinda, chirichonse kudutsa mdziko chimayenera kuti chithandizire misonkhano yanga kapena ine sindipitako. Uko nkulondola. Chabwino, tangoganizani. Ine ndikuganiza kuti kuli mwinamwake mipingo yaikulu ya Baptisti sikisite kapena sevente mu Louisville momwe. Mukuona? Nanga bwanji Amethodisti? Ndipo ndi tauni ya Amethodisti; Asbury ali kuntunda uko. Kodi munthu ameneyo angakhale ndi chiyani ngati iye atabwera ku mzinda uno, wa Amethodisti ndi Abaptisti okha, ngakhale Apresbateria ndi onse?”

¹⁶ Tsopano ndi mipingo ingati ya Uthenga wathunthu imene ili muno mu mzinda? Mamishoni awiri kapena atatu kumusi kuno kwina kwake, mipingo yaing’ono chabe, apa ndi apo, ndipo iwo ili pa nkondo wina ndi mzake.

¹⁷ Chotero pamene iwe ukubwera, umayenera kuti uziyima pa mphamvu ya utumiki wako. Uko nkulondola. Ndipo ngakhale... aliyense ali ngati ndale zikulowamo. Izo zimatengera mphamvu ya utumiki wako, kuti uzitengako kuchokera ku chirichonse chimene Ambuye angamatumize. Ine ndimazikonda izo mwanjira imeneyo. M’bale, ngati Yesu Khristu sali pokhalapo panga kuno, ndi podalirapo panga, ndiye ine ndiribe china chirichonse choti ndizichidalira. Uko nkulondola. Iye... Pa Khristu, Thanthwe lolimba, ine ndaimirira; maziko ena onse ndi mchenga wotitimira, kwa ine. Ine kulibwino kuti ndizilalikira kwa anthu faivi amene ine ndikudziwa kuti Mulungu anawatumiza kuti adzamve Uthenga, kuposa kumalalikira kwa teni sauzande amene anakokeredwa mwa ndale mmenemo. Uko nkulondola.

18 Ine kulibwino ndiziwona kutembenuka kumodzi kwachikale, kufika pa guwa ndikumati bhuu-uuu ponsepo, kuposa kuti ndiziwona teni sauzande atayima, akungoti, “Chabwino, ine ndiyesera Izo.” Kuyesera Izo? Iye si Khristu woti muzimuyesera. Iye ndi Mmodzi woti muzimulandira. Kukhala moyo kapena kufa, kumira kapena kumizidwa, muzimutenga Iye mulimonse. Uko nkulondola.

19 Ngati ine ndingapemphere, kuwapempherera anthu teni sauzande usikuuno, ndipo iwo onse nkufa mmawa; mawa usiku ine ndingabwerere kuno kumadzawapempherera odwala, ndikumakhulupirira kuti Mawu a Mulungu anali olondola. Izo nzoona.

20 Ngati ine nditati ndikufa; ndipo anthu faivi sauzande anafa zaka handiredi zapitazo, ndipo akhala ali ku Umuyaya motalika chomwecho, atati awuka ndipo nkubwerera ku dziko lapansi, ndipo nkudzati, “M’bale Branham, inu musadalire Iwo. Iye sakulondola. Musadalire Iwo. Ife—ife tinkamudalira Iye, tinapita; tinalephera.”

21 Ine ndinganenebe, “Ndiloleni ine ndife mwa Yesu Khristu.” Uko nkulondola. Ine ndikuwakhulupirira Iwo. Ndipo ndiwo mtima wanga wonse, chirichonse chayikidwa pomwepo mwa Iwo. Ndipo ine ndimawakhulupirira Iwo ndi mtima wanga wonse, ndipo ine ndimadalira pa Iye.

22 Ndipo ine ndimawakonda anthu Ake. Ine ndimakukondani inu, nzika zimzanga za Ufumu wa Mulungu. Ndipo ine ndikufuna kuti ndiziyima phewa ndi phewa ndi inu, ndipo kuzenza mtolo.

23 Tsopano, usikuuno; ine ndinapereka, usiku watha, ine ndimati ndiyankhule kanthawi pang’ono usikuuno, Ambuye akalola. Sindikufuna kukusungani inu motalika kwambiri, kukutopetsani inu, chifukwa ife tikuyembekezera . . .

24 Ine ndiri ndi ngati chikopa cha ubweya pamaso pa Ambuye pa msonkhano uno. Ndipo ine ndikuyembekezera kuti Mulungu achite chinachake chimene chiti chiyambitse msonkhano kugudubuzika komwe kuno mu mzinda. Inu mupemphere, murchite gawo lanu; ndiye, pamene Chiweruzo chidzabwera, ife tonse tidzathe kuima ndi kunena kuti tinachita gawo lathu.

25 Mu mutu wa 20 wa Eksodo, ndipo kuyambira ndi ndime ya 7, ine ndikufuna kuti ndiyankhule mphindi pang’ono chabe, ngati Mulungu alola, pa . . . chabwino, ine ndingatati, osati phunziro lapadera, koma a—phunziro labwino. Lamlungu lathali, pa Sande sukulu ku kachisi mu Jeffersonville, ife tinayamba, pa, “chiwombolo mwa Magazi.”

26 Ndipo pano ndi chimene ine ndikuyesetsa kuti ndichite, ngati inu mukufuna kuti mudziwe chifukwa chimene ine ndikuchitira izi pano. Ambiri a inu mukuti simunandiwonepo

ine ndikulalikirira mu msonkhano wamachiritso, koma ndi kwa cholinga. Ine ndikuganiza, ngati ine ndingapangitse miyoyo kusweka ndi kubwera pa guwa, ndiye ine ndingapeze kukonderedwa ndi Mulungu kwa Louisville, uko nkulondola, pamene anthu afika pansu kwenikweni pamaso pa Mulungu ndi kumapemphera.

²⁷ Ndipo, kenako, pali ambiri a inu, azimzanga, amene mukumapemphera, kusala kudya, ndipo nkumawopa kutenga chimene mukuchipemphereracho. Uko nkulondola. Mukuona? Chabwino, izo sizingakuchitireni inu ubwino uliwonse kuti muzisala ndi kumapemphera, pokhapokha ngati inu muli ndi ntchito zina zoti zitsatire izo. Chikhulupiriro chanu chonse, padziko lapansi, sichingakuchitireni inu ubwino uliwonse pokhapokha ngati inu mutatuluka kunja uko, ndi kukakumana molunjika ndi izo, ndi kutenga izo. Ndizo zonse. Inu mukuyenera kupita patsogolo. Inu mukuyenera kungotuluka ndi kuchita izo, mulimonse. Mukapempha chirichonse, muzipita kukachitenga icho. Mulungu anati ndi zanu, chotero musamatenge chirichonse chochepera. Muzitenga chimene inu munachipempha. Inu muzichita zimenezo, ndipo muwone momwe izo zimatulukira. Eya. Musati—musamabwerere mmbuyo ndikuti, “Chabwino, nditenga chachiwiricho.”

²⁸ Nditenga choyamba. Mulungu anandilonjeza ine, choyamba, ndicho chimene ine ndikuchifuna. Ndipo kwa zaka twente-firii izi zimene ine ndamutumikira Iye, Iye wandipatsa ine malo amenewo. Ndipo ine...Ndipo bola ngati ine ndikumukhulupirira Iye ndi kumukonda Iye, ndipo Iye amandikonda ine, izo zidzakhala mwanjira imeneyo basi chifukwa Iye ndi wokakamizika ku Mawu Ake. “Chirichonse chimene inu muchikhumba, pamene mupemphera, khulupirirani kuti mwachilandira icho, inu mudzakhala nacho icho.” Ndicho chimene Iye ananena. Nkulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Izo nzabwino. Chabwino.

²⁹ Ine ndimakonda kumakumvani inu mukamanena, “Ameni.” Inu mukudziwa, Mlongo Hoover, *ameni* amatanthauza “zikhale chomwecho,” kwa ine, inu mukudziwa. Ndipo ine—ine ndikayamba kuyankhula, ine ndikapanda kumumva wina akunena “ameni,” ine—ine ndimadabwa nazo.

³⁰ Kuno nthawi ina kale ine ndinkalalikira mu tchalitchi chaching’ono, ndipo—ndipo ndinali basi...Oh, ndiribe mwambo wa paguwa wambiri, molingana ndi, ine ndikuganiza, zaumulungu za tsikuli, chotero ine ndikuganiza ine ndinakhala wosalamulirika pang’ono. Ndipo ine ndikuganiza ine ndinadumphira mmwamba pa nsanja pa guwa, monga *choncho*, ndipo ndinadzagwira maikrofoni mdzanja langa, ndikudzakhala pamenepo, ndipo mapazi anga akugwedezeza, ndikulalikirira molimba basi monga ine ndikanathera. Ine ndinatsitsimuka; ine

sindimadziwa chimene ine ndimachita. Mu maminiti pang'ono, ndinabalalikanso, ndipo ndinadzipeza ndekha ndiri pansi pakati pa kanjira, ndikukwezera miyendo ya thalauza langa. Ine sindikudziwa chifukwa chake, koma ndinali kwenikweni... Ndikanakonda ndikanakhala pamenepo kwa kanthawi. Ndicho chinthu chimodzi chimene ndikufuna kuti ndinene. Panali penapake pamene ine ndithudi ndinkasangalala ndekha. Ndinangokhala moyo pakudya izo kwa masiku angapo zitatha zimenezo.

³¹ Apo panali munthu anadza kwa ine, ndipo iye anati, “Anati,” iye anati, “inu mungalalikire bwanji, ndipo anthu onse amenewo nkumati, ‘Ameni?’”

Ine ndinati, “Ndizo zimene zimandipangitsa ine kumalalikira.” Eya.

³² Ine ndinkakonda kukhala ndi galu wokalamba. Ndinkasaka mbira. Ine ndikuganiza ndiri ndi abwenzi ambiri aku Kentucky pano amene amakonda kusaka mbira. Chotero...Ndipo iye ankathawitsira mu mtengo chirichonse chimene chinalipo, ndipo amapita kukagwira icho, pambali pa kanyimbi; ndipo iye analibe chochita ndi zimenezo. Tsopano, iye ankamuthamangitsira iye pansi pa mulu wa tchire. Ndipo chinthu chokhacho chimene ine ndinkayenera kuti ndichite, ine sindinkafuna kuti ndilowe pansi pamenepo kumutsatira iye, ine ndinali wotsimikiza. Chotero chinthu chokhacho chimene ine ndinkachita, ndi kungodzutsa tchirelo, ndi kumamusisita iye ndi kufuula, “Mugwire iye, mnyamata! Mugwire iye!” Ndipo iye ankapita kukamugwira kanyimbi.

³³ Tsopano kanyimbi woyipa kwambiri amene ine ndimamudziwa ndi mdierekezi. Ndipo ngati inu mukufuna kuti muzisisita pang'ono, musingofuula “ameni” kamodzi mu kanthawi. Ndipo ine—ine...Ife timamuthamangisira iye mu mtengo, pakapita kanthawi, ndi kupita kukamugwira iye. Mukuona?

³⁴ Inu mukudziwa, Buddy Robinson wakale, ambiri a inu munamvapo za iye. Sichoncho inu? Mpingo wa Nazarene. Iye anati, “Ambuye,” anati, “ndipatseni nsana wonga chipika cha macheke. Ndipatseni ine chidziwitso chochuluka ku mapeto a moyo wanga. Ndipo mudirole ine ndimenyane ndi mdierekezi bola ngati ine ndiri ndi dzino limodzi, ndipo kenako kumupana iye kufikira ine ndife.” Ndikuganiza kuti izo nzabwino... Ndipo ndicho basi chimene iye anachita. Ndizo basi zomwe iye anachita; kutali, pafupifupi zaka handirede zakubadwa, ndipo akulalikirabe Uthenga.

³⁵ Ine ndimawamva asilikali akalewo akulalikira monga choncho. Tsiku lina, ndinapezeka nditatsegula wailesi, ndipo m'bale wokalamba, dzina lake Mordecai F. Ham, pafupifupi zaka handirede zakubadwa, akumalalikirabe Uthenga. Ine

ndinati, “Mulungu, mdalitseni iye, ndipo mulole iye akhale ndi nyenyezi mu korona wake pamene iye adzafika Kumeneko.” M’bale Ham, ine sindimamudziwa iye. Limodzi la masiku awa ine ndikufuna ndidzakomane naye iye asanawoloke, Dzikolo. Ndipo, chotero, iye akhoza kudzagwirana chanza ndi anthu ambiri Kumeneko. Ine ndikudziwa iye adzakhala nawo ochuluka oti agwirane nawo chanza pamene iye adzafika Kumeneko, oh, chifukwa iye wakhala ali msilikali wakale.

³⁶ Ambuye akudalitseni inu tsopano. Ndipo tsopano, ife tisanalowe mu Mawu awa, tiyeni timupemphe Mlembi kuti atsikire kuno ndipo adzawaululire Iwo kwa ife.

³⁷ Atate athu Akumwamba achifundo, ife tikukuyandikirani Inu, usikuuno, mu Dzina lokondeka lija, lopambana la Mwana Wanu, Yesu; kuvomereza machimo athu, kuti si ife oyenera kuyankhula Dzina Lake loyera. Pakuti mu...Banja lonse la Kumwamba limatchedwa “Yesu.” Banja lonse padziko lapansi limatchedwa “Yesu.” Ndipo mu Dzina limenelo bondo lirilonse lidzagwada, ndipo lirime lirilonse lidzavomereza Ilo, kaya iwo ndi ochimwa kapena ojera mtima. Ndiye, pamene ife tiyankhula mu Dzina Lake, momwe ife tikuyenera kumanjenjemera mmitima yathu, ndi kulemekeza, pamene ife tikuyankhula. Chotero ife tikupempha mu Dzina Lake, molemekeza, kuti Inu mubwere kwa ife usikuuno, Ambuye.

³⁸ Ife tiri pano pakati pa mzinda waukulu, ndi mitundu yonse ya zida zimene Satana wawamangira nazo anthu, mu mabizinesi awo, mu njuga zake, ndi uchiwerewere, mowa, ndi ndudu. Ndipo, O Mulungu, ndi atumiki ambiri, pa guwa, mungolola izo zidutse ngati kuti chinali chimodzi cha zinthu wamba.

³⁹ Koma, Mulungu, tipatseni ife liwu la chenjezo, kuti ife tizilalikira Uthenga molunjika ndi moona, kuyika nkhwangwa ku muzu wa mtengo, kulola zidutswa zigwe paliponse pamene ziti zikhale. Koma tithandizeni ife, Ambuye, kuti tizilengeza chiweruzo pa zinthu zoterozo, ndi kulalikira Uthenga wa Mwana Wanu wokonedwa, Yesu.

⁴⁰ Mulungu, mupereke kuti chinachake chichitike chimene chiti chidzagwedeze mzinda uno kwa Ufumu wa Mulungu. Kuti, ngakhale mipingo, imene ikungopitirira pa ngodya, ndi mamembala ochepa, O Mulungu, mulole mipingo imenayo idzaze ndi kudzaza ndi anthu abwino, akachitidwe-kachikale, ojera, obadwa mwatsopano. Perekani izi, Ambuye. Ndipo mulole ife tilandire chitsitsimutso, chitsitsimutso chachikale, chotumizidwa ndi Mulungu chimene chidzangogwedeza kuchokera mbali imodzi ya mzinda kupita ku yina, kuchotsa kuyipa konse. O Mulungu, musatipatse ife msonkhano wotalikirapo. Mutipatse ife chitsitsimutso chimene chiti chitseke malo ogulitsiramo mowa, ndi chimene chiti chidzakonze zinthu; ndi kuwapangitsa anthu kubwera, pamene mabelu a tchalitchi

alira, ndi kudzakhamukira ku guwa ndi kumapemphera uthenga wa abusa usanabwere, ndi kukonzeka. Mulungu, perekani izi.

⁴¹ Tsopano, usikuuno, pakhoza kukhala odwala pano, Atate. Ndipo pamene ife tikuyankhula za odwala, kapena kwa odwala, aponso, mulole Mzimu Woyera uchize munthu wodwala aliyense mnyumba muno. Mupulumutse wochimwa aliyense. Muwaitane abwerere, kunyumba, wobwerera mmbuyo aliyense kuchoka ku njira yake yobwerera mmbuyo.

⁴² Ndipo tsopano mulole Mzimu Woyera ukhale Umodzi umene wanditsogolera ine ku phunziro ili, usikuuno. Ndipo mulole Iye atenge zinthu za Mulungu ndi kungomugwiritsa ntchito wantchito Wake pano ngati chida, ndipo mulole Mulungu alandire ulemelero. pakuti ife tikupempha izi mu Dzina Lake. Amen.

⁴³ Mu ndime ya 7 ya mutu wa 20 wa—wa Numeri, timawerenga izi.

Ndipo AMBUYE anayankhula kwa Mose, anati,

Tenga ndodo, ndipo usonkhanitse gulu pamodzi, iwe, ndi Aroni m'bale wako, . . . uyankhule kwa thanthwe pamaso pawo; ndipo ilo lidzatulutsa madzi ake, . . .

⁴⁴ Ine ndikufuna inu muzindikire, madzi “Ake”.

. . . ilo lidzatulutsa madzi Ake, ndipo iwe udzawatulutsira iwo madzi kuchokera mu thanthwe: chotero iwe udzapereka kwa gululo ndi nyama zawo akumwa.

Ndipo Mose anatenga ndodo pamaso pa AMBUYE, monga anamulamulira iye.

Ndipo Mose ndi Aroni anasonkhanitsa khamu lonse ku thanthwe, ndipo iye anati kwa iwo, Imvani. . . opanduka inu; kodi ife tikutulutsireni madzi kuchokera mu thanthwe?

Ndipo Mose anakweza mmwamba dzanja lake, ndipo ndi ndodo yake anamenya thanthwe kawiri: ndipo madzi anaturuka mochuluka, ndipo khamulo linamwa, ndi nyama zawonso.

⁴⁵ Ambuye atenge Mawu ochepa awa tsopano, pamene ife tikubwerera ku phunziro lathu la usiku watha ndi kulibweretsa ilo ku ili, Mulungu akalola.

⁴⁶ Ndipo tsopano, ine ndikufuna odwala onse amene ali muno, usikuuno. . . Tsopano, Billy sanapereke konse makadi apemphero aliwonse lero, chifukwa ine ndinamuuza iye kuti asatero. Ine ndinati, “Ungopita, Billy, ndipo ukamuuze M'bale Cauble. Ndipo ungondilola ine. . .”

⁴⁷ Ine ndikuyesera chinachake, kwa ulemelero wa Mulungu. Tingomupempha Mulungu kuti atithandize ife, kuti atipatse

ife miyoyo mu Ufumu; ndi okhulupirira amene ati alimbikitse chikhulupiriro chawo, ndi kusunthira mmwamba, ngakhale popanda china chirichonse, amangosunthira mmwamba ndikuti, “Mulungu, ine ndikukukhulupirirani Inu, pa Mawu.” Ndi zimenezotu. Imeneyo ndi njira yoyambirira, ndipo yoyamba, ndipo yabwino kwambiri. Uko nkulondola. Mumutenge Mulungu pa Mawu Ake. Ndiye, ngati inu simungachite zimenezo, ndiye, ndithudi, Mulungu atumiza zinthu zina, monga ngati mphatso ndi zizindikiro, kuti—kuti zikatsimikizire Mawu Ake, kuti zikawatsimikizire Iwo kwa wokhulupirira aliyense.

Tsopano, Lamlungu, ife tinali ndi, “chiwombolo mwa Magazi.”

⁴⁸ Ife tikumutenga Israeli tsopano, mu ulendo wawo, akutuluka mu Igupto, choimira cha dziko lapansi, ali pa ulendo wawo waku Palestina, dziko lolonjezedwa. Ine ndikuganiza kuti icho ndi chinthu chokongola. Ine ndimangochikonda icho. Pafupifupi sabata iliyonse, ine ndimakhala pansu ndi kumawerenga Bukhu la Eksodo limenelo, ngati ine ndingathe, kapena zochulukwa za izo momwe ine ndingathere. Ine ndimalikonda ilo chifukwa ndi choyimira changwiwo cha mpingo lero, chikhalidwe, ndi momwe Mulungu akusunthira. Anasuntha ndiye, chimene Iye anachichita mu thupi pamenepo, Iye akuchichita mu uzimu tsopano. Mukuona izo?

⁴⁹ Tsopano, pamenepo Iye anatsogolera Israeli, mthupi, kumene iwo anawona, anayang’ana, anawasuntha iwo kuchokera ku dziko lina kupita ku dziko lina la chithupi.

⁵⁰ Tsopano ife timasunthidwa ndi Mzimu Woyera, popita tsopano mu Dziko lolonjezedwa. Kodi inu mukukhulupirira kuti ife tiri pa njira yopita ku Dziko lolonjezedwa? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. “Mu nyumba ya Atate anga muli malo ambiri. Ngati zikanakhala kuti siziri chomwecho, Ine ndikadakuuzani inu. Ine ndipita ndi kukakukonzerani inu malo.” Nkulondola uko? [“Ameni.”] Tsopano ife tiri ndi Dziko lolonjezedwa limene ife tikupitako, ndipo tsiku lililonse limapanga chochitika chachikulu; tsiku lina, chochitika chachikulu china.

⁵¹ Ndipo pali mthunzi waukulu wakuda uli kutsidyako patsogolo pathu, wotchedwa imfa. Ndipo nthawi iliyonse pamene mtima wathu ugunda, timasunthira sitepe imodzi kuyandikira kwa iwo. Limodzi la masiku awa, iwo udzagunda komaliza, ndipo tidzakalowamo. Ine ndikufuna kuti ndidzakhale pa nthawi yanga, kudzapanga gawo langa; monga ine ndikuyembekezera mmodzi aliyense wa inu ali, usikuuno. Pamene ine ndidziwa kuti iwo uli patsogolo panga basi, ndipo ine ndikuyenera kuti ndikumane nawo, ine sindikufuna kuti ndidzakhale wamantha. Ndikufuna kuti ndidzadzikulunge ndekha mu mwinjiro wa chilungamo Chake, ndikuyenda

kukalowa mmenemo, ndikudziwa ichi, kuti ine ndikutsimikiza kuti ine ndikumudziwa Iye mu Mphamvu ya chiwukitsiro Chake. Uko nkulondola. Kuti, pamene Iye adzayitana kuchokera kwa akufa, ine ndidzayitanidwa ndi iwo amene ali moyo. Mulungu ndi Mulungu wa amoyo.

⁵² Tsopano, pamene iwo ankayenda mu dziko ili, ife tikupeza kuti Mulungu anapanga—anawapangira iwo dongosolo. Iye anabweretsa chiwombolo, mwa magazi. Ndiye ife tikupeza kuti, Iye akubweretsa chiwombolo, kachiwiri, mwa mphamvu.

⁵³ Ife tinapeza, usiku wadzana, kuti Iye anali atapaka magari; chimene chinali choyimira chokongola kwambiri cha wokhulupirira, kuti, pamene iye wavomereza imfa ya Khristu mmalo mwake, ndiye iye amadzakhala mwana wa Mulungu. Iye amayamba pa ulendo wake.

⁵⁴ Tsopano, chinthu chotsatira chimene iye akuyenera kukhala nacho. . . iye atapulumutsidwa, mwauzimu.

⁵⁵ Tsopano, imfa ya mwanawankhosa wosalakwa inkapereka moyo kwa wokhulupirira wolakwayo. Kodi chimenecho si choimira changwiro tsopano? Imfa ya Wosalakwa, ikupereka Moyo kwa wolakwa. Ndipo imfa ya Khristu wosalakwa imapereka Moyo kwa ife olakwa.

⁵⁶ Tsopano, choyamba, ndiye, Mulungu atatha kuwapatsa iwo moyo kudzera mmagazi, ndipo nkutsimikizira izo, kuti imfa inawadutsa iwo, Iye anawayambitsa iwo mu ulendo wawo. Ife tikumanizana nawo iwo pakapita kanthawi.

⁵⁷ Tsopano zindikirani, ndiye, chinthu chotsatira chimene Mulungu anachita, mwamsanga pamene iwo anadzakhala okhulupirira ndi ana, ndipo namulandira Mulungu, mdani wa imfa ya thupi anawatsatira iwo. Ndipo iye anawayika iwo pangodya, pomwepo; ndi chipululu mbali imodzi; Nyanja Yofiira mbali inayo; mapiri mbali ina; Gulu lankhondo la Farao likubwera, kumawatsatira, asilikali mamiloni akubwera mu kuguba, kuti adzawagonjetse iwo.

⁵⁸ Tsopano, Mulungu anali atawonetsera kuti Iye anali atawapatsa iwo moyo, kudzera mu imfa ya mwanawankhosa; tsopano Iye awawonetsa iwo chiwombolo chathupi. Aleluya! Mwaona, ziwiri zonse kwa chipulumutso ndi machiritso, mwaona, kwa munthu wachirengedwe ndi munthu wauzimu.

⁵⁹ Mngelo wa imfa anadutsa, kutsimikizira kuti Mulungu anali atakonzana njira yopulumukirapo, kudzera mu kupereka nsembe ya magari, ndipo iwo anailandira iyo. Tsopano Iye adzapanga njira yopulumukirapo kwa imfa ya thupi.

⁶⁰ Monga wokhulupirira, mwamsanga pamene iye apulumutsidwa. Mwinamwake khansa yamudya iye, kapena nthenda yina. Mulungu amakhala nacho chiwombolo, aponso, kudzera mu mphamvu. Chimodzimodzi monga Iye ali nacho

chiwombolo cha moyo, Iye ali ndi chiwombolo cha thupi. Icho chinali a . . .

⁶¹ Iwo anapulumutsidwa, ndipo iwo anadulidwa. Iwo anali pansu pa magari, koma, komabe, Farao ankapita . . . Mdaniyo ankapita kuti akawawononge iwo, akawaphe iwo onse pomwepo mchipululu, kenako Mulungu anawonetsa mphamvu Yake ya chiwombolo kwa thupi lawo. Inu mukumvetsa zimenezo? Inu mukuchidziwa chimene ine ndikunena? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Chiwombolo mwa mphamvu! Ndipo kenako, pamene mdani anali pafupi pomwe pa iwo, Lawi la Moto lalikulu lauzimu linawuka kuchokera pa Israeli, linadzabwera cha kuno ndipo linadzaima pakati pa iwo ndi imfa.

⁶² Mulole izo zilowerere kwa maminiti pang’ono. Kodi inu mukutha kuwona chimene ine ndikunena? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi].

⁶³ Tsopano, kwa wokhulupirira aliyense, mwana wobadwamwatsopano wa Mulungu, pamene imfa ibwera kuzaba pa chitseko, nthawi isanakwane, Mngelo wa Mulungu amaima pakati pa inu ndi nthendayo. Tsopano, ngati inu mukufuna kuti muthamangire kumene kuli iyo, imeneyo ndi ntchito yanu; koma inu simukusowa kutero. Mukuona? Iye wayima pakati pa inu ndi imfa.

⁶⁴ Zaka twente-firiri zapitazo, mu Chipatala cha Chiyuda, Dr. Morris Fletcher anandipatsa ine maora atatu; mmodzi wa madokotala anu a oparesoni apamwamba kuno mu mzinda, anandipatsa ine maora atatu okhala moyo. Ine ndiri wamoyo, usikuuno. Alaluya! Bwanji? Mwa chisomo chosandiyenera, Mngelo wa Mulungu anayima pakati pa ine ndi imfa, kuti anditeteze ine, ndipo ine ndinavomereza Izo. Ndipo poyamikira, mwa chisomo cha Mulungu, ine ndapindulira miyoyo theka la miliyoni kwa Iye, usikuuno.

⁶⁵ Oh, momwe Mulungu amadziwira kuchita zinthu, ngati ife tingamangotsatira. Musamayesere kumamutsogolera Mulungu. Mulole Mulungu azikutsogolerani inu. Mukuona? Ife ndi amene tikuyenera kuti tizitsogoleredwa. Ine ndikuganiza kuti ndi chifukwa chimene Mulungu anatifanizira ife ndi nkhosa.

⁶⁶ Kodi inu munayamba mwaiwonapo nkhusa itatayika? Bwanji, iyo ndi nyama yopanda thandizo kwambiri mdziko. Iyo siimadzipezera njira yake paliponse. Iyo imangoyima ndi kumaphiriphita kufikira nkhandwe itamudya iye, kapena iyo imafera pamenepo. Iyo siimapeza njira yobwerera mmbuyo.

⁶⁷ Ndipo ndiyo njira, imene, pamene munthu watayika, iye amakhala wopanda thandizo kwathunthu. Palibe chimene inu mungachite za izo. Mulungu, kupyolera mu chisomo, akuyenera kumakutsogolerani inu kwa Khristu. Yesu anati, “Palibe munthu angadze kwa Ine pokhapokha Atate atamukoka

Iye. Ndipo onse amene Iye awakoka, ndipo nkubwera, Ine ndidzamupatsa iye Moyo wosatha.” Ndi lonjezo bwanjii!

⁶⁸ Oh, ine ndikukhumba ndikanamubweretsa munthu aliyense muno, izo nkumatsikira pansi pa nthiti yachisanu ku mbali ya kumanzere, mpaka izo zitagunda mkati mwa mtima. Inu mukanawawona anthu akumangonyamuka, ali ndi mitundu yonse ya matenda ali pa iwo, akutuluka mchipinda chino, akusangalala, akukana kukhala nawo iwo. Olumala akanamayenda bwino bwino momwe iwo akanathera. Iwo akanamakana kudziwa china chirichonse. Mukuona?

⁶⁹ Inu mukuchita mantha. Mukuopa kuti muyambepo. Mukuyembekezera kuti Mulungu atsike pansi ndipo adzakukokeni inu. Mulungu samachita zimenezo mwanjira imeneyo. Inuyo ndi amene mukuyenera kuti mupange sitepe. Iye amapereka lonjezo, ndipo amati, “Bwera,” ndiye inu mumatsatira.

⁷⁰ Tsopano zindikirani ana a Israeli, ndiye. Mulungu anabwera ndipo anadzaima pakati pa iwo ndi chowopsyacho; mphamvu ya chiwombolo . . . chiwombolo mwa mphamvu, kani. Chiwombolo mwa magazi; chiwombolo mwa mphamvu.

⁷¹ Usiku watha tinawasiya iwo, akungokwawira pa gombe, tsidya lina la Nyanja Yofiira. Adani onse, magudumu awo a magaleta anali atagulukapo. Akavalo awo ananjenjemera ndi mantha, pakati penipeni pa mtsinje, ndipo iwo anali akutembenukira mbali iliyonse, akupita njira *iyi*, ndipo magudumu anatitimira mmatope ndipo anagwa. Ndipo gulu la anthu linkamuthawa mwamantha, mdaniyo. Ndipo Israeli anakwera pa gombe, kuti amuwone Mulungu akutambasula dzanja Lake ndi kuwononga mdani aliyense.

⁷² Choimira chokongola, wokhulupirira, pansi pa Magazi; atachiritsidwa pamenepo ndi mkhala-pakati, mphamvu ya Mulungu ikusunga moyo wake, kuwutalikitsa iwo kwa kanthawi. Iwo akanakhala, wina aliyense, ataphedwa apo pomwe; iye akanawapha iwo mchipululu momwemo, Mulungu akanapanda kuyima pakati pawo. Ine ndikanafa, kalekale, ngati Mulungu akanapanda kuyima pakati pa ine ndi imfa. Wokhulupirira aliyense muno akanakhala atamwalira, kalekale, ngati Mulungu akanapanda kuyima pakati pa inu ndi imfa; aliyense wa inu. Chotero, Mulungu, mu chisomo Chake chochita mwayekha ndi chifundo, wayima pakati pa wokhulupirira ndi imfa. Aleluya!

⁷³ Ndi ichi apa. Ndiye chinthu chotsatira kwa wokhulupirira ndi chiyani? Chinthu chotsatira ndi ubatizo wa Mzimu Woyera. Mose anawatsogolera ana a Israeli mpaka ku Nyanja Yofiira, anabatizidwa mu Nyanja Yofiira. Nyanja, madzi, akuyimira Mzimu. Pamene iye anamenya Thanthwe, madzi anaturukamo. Ndipo ilo linali choyimira cha Khristu, mu Yohane 3:16.

“Mulungu anakonda dziko lapansi, Iye anapereka Mwana Wake wobadwa yekhayo, kuti aliyense amene akhulupirira Iye asatayike, koma akhale ndi Moyo wosatha.” Zindikirani, anthu owonongeka, mu chipululu, anapulumsidwa ndi Thanthwe lokanthidwa. Ndipo anthu owonongeka akupulumutsidwa lero (kuwonongeka mu tchimo, kuwonongeka mu kusaeruzika) chifukwa Mwana wokanthidwa wa Mulungu anatenga malo awo; madzi, Mzimu, zikutuluka!

⁷⁴ Penyani, ine ndikufuna inu muwone izo tsopano, pamene iwo ankadutsa mu Nyanja Yofiira, chinali choyimira cha kulandira Mzimu Woyera. Wokhulupirira atawomboledwa ku imfa, kupita ku Moyo; mphamvu ya Mulungu yachiritsa thupi lake; tsopano iye amakhala woti abatizidwa ndi Mzimu Woyera. Tsopano iye ali ndi ulendo, uko, patsogolo pake; koma, iye asanakumane ndi ulendo umenewo, iye akuyenera kukhala ndi chinachake choti chimunyamule iye akafikeko. Amen. Choimira changwiwo cha Pentekoste!

⁷⁵ Zindikirani, pamene iwo ankakwawa kuchoka pa gombe. Wokhulupirira aliyense, pamene inu mubwera ndipo mwapulumutsidwa, mwalandira Magazi a Yesu, inu mumayeserabe kukangamira pa *ichi* ndi kukangamira pa *icho*, ndipo simukutha kusiya *ichi* ndipo simukutha kusiya *icho*. Pakapita kanthawi, Mulungu akhoza kumakuchitirani inu zinthu zabwino; koma inu osatha kusiya ndudu zanu, inu mumafuna kuti muzimwa chakumwa chosangalatsa ndi azimzanu nthawi ndi nthawi. Koma chimene inu mukusoweka kuchita ndi kudutsa Nyanja Yofiira.

⁷⁶ Pamene iwo anatulukira mbali yina. Ndi izi apa. Ine ndikufuna kuti inu muwone chimenecho. Pamene iwo anatulukira tsidya linalo, anakwawira pa gombe ndipo anayang’ana mmbuyo, ndipo anawawona ogwiritsa ntchito akale onse awo amene ankawakwapula iwo, nkuwapha ena a iwo. Monga ngati khansa ndi ndudu ndi fodya ndi mowa ndi china chirichonse, zimawapangitsa ana misala, zimawatumiza iwo ku malo opulumukirako, mu zipatala, ndi gulu la amisala ndi china chirichonse chimene chimapezeka mdziko. Pamene iwo anayang’ana mmbuyo ndipo nkuwona zinthu zonsezo akuvutika, opanda thandizo, ndipo akufa mu nyanja. M’bale, inu mukukamba za msonkhano; iwo anali nawo umodzi!

⁷⁷ Mose! Oh, ine ndilola izi kuti zizame mwakuya. Ine ndikuyembekeza izo zikupita pansu. Mose, mneneri wamkulu kwambiri amene anayamba wakhalapo, kunjwa kwa Yesu Khristu. Panalibe munthu amene Mulungu anayamba wayankhulapo naye, monga Iye ankachitira ndi Mose, kunjwa kwa Khristu. Iye anati, “Ngati pakhala mmodzi amene ali wauzimu, kapena mneneri, pakati panu, Ine ndimamuwonetsa iye masomphenya ndi kuzizindikiritsa Inemwini kwa iye. Koma

osati mtumiki Wanga Mose; Ine ndimayankhula naye iye mlomo ndi khutu.” Uko nkulondola.

⁷⁸ Mose, munthu wolemekezeka uyu. Mwamsanga pamene iye anadutsa mu chomuchitikira chimenecho, iye anawawona ogwiritsa ntchito onse aja atafa, iye ankadziwa kuti zinthu zonsezo zinali zitapita kwanthawizonse pamenepo. Zinthu zonsezo zimene zinkawathamangitsa iwo, ndi kumawamenya iwo, ndi kumawakwapula iwo pamenepo, zinali zitatha. Iye anakweza manja ake ndipo anayimba mu Mzimu. Oh, mai!

⁷⁹ Sizinayambe zayimiridwapo, ndipo sizidzatero, mpaka ife tidzafike ku Ulemelero uko. Pamene kumaliza kunapangidwa kumeneko, iye anayimba mu Mzimu. Ndipo pamene ife tawomboledwa mu thupi. . .

⁸⁰ Icho chinali choyimira cha Mzimu Woyera ukubwera pa Pentekoste, pamene ife tinkadutsa pa nyanja. Icho chinali choyimira cha Pentekoste. Ndipo Mose, mu chotsu. . .mu choyimira kumbuyo uko, pamene iye ankadutsa mu zimenezo, iye anayimba mu Mzimu. Iwo unabwera pa Tsiku la Pentekoste. Ndipo pamene thupi likhala langwiro, lowomboledwa. . . Tsopano solo yathu ndi yowomboledwa mwangwiro, chabwino, “singawonongeke; ili ndi Moyo wosatha.” Chimene Baibulo limanena!

⁸¹ Oh, ine ndikumverera bwino. Zindikirani chifukwa chake. Chifukwa ine ndikudziwa kuti ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Mungozika solo yanga pamenepo, ndipo nkumayendabe, ndi kuti, “Satana, ungouzira zonse zimene iwe ukufuna, kwa ine. Usandivutitse ine, chifukwa ndikumudziwa Amene ine ndamukhulupirira, ndipo ndiri wokakamizika kuti Iye ndi wokhoza kusunga icho chimene ndachipereka kwa Iye kufikira Tsikulo.” Ameni.

⁸² Chimene ife tikusowa usikuuno ndi chitsitsimutso chabwino, cha kachitidwe- kachikale, cha Billy Sunday, chosweka, cha aleluya, ndi chimene ife tikusowa kuzungulira Louisville kuno. Uko nkulondola, tikusowa chitsitsimutso chabwino, chachikale, cha chipentekoste chotumizidwa ndi Mulungu. Inde, bwana.

⁸³ Zindikirani, ndiye, pamene matupi athu awomboledwa. . . Chimene, ife tiri ndi machiritso Auzimu tsopano, ngati mthunzi.

⁸⁴ Monga iwo unali mthunzi kumeneko wa Pentekoste, onani chimene iwo anachita mu nthawi ya mthunzi, ya chipulumutso. Taonani momwe iwo anayendera kumeneko pamaso pa Mulungu, “Anazimitsa. . .mmphepete ndi zina. . . moto, ndi kuthawa lupanga lakuthwa,” zinthu zonsezi zimene iwo anazichita, “anatuluka mu ng’anjo zamoto; kutali ndi denje la mikango, ndi chirichonse,” mwa mthunzi, aleluya, mwa mthunzi wa Pentekoste.

⁸⁵ Tsopano ife tiri ndi chiwombolo changwiro kudzera mu Magazi a Khristu. Iwo sakanakhala ndi chiwombolo

changwiwo nthawi imeneyo, chifukwa icho chinali pansu pa magazi a ng'ombe ndi mbuzi, ndipo iwo samachotsa tchimo; iwo ankangophimba tchimo. Koma pamene Magazi a Yesu anakhetsedwa, Magazi opatulika olungama kwambiri, machimo sanaphimbidwense; iwo anasudzulidwa ndipo anathetsedwa, ndipo wokhulupirira amapita mu Kukhalapo kwa Womupanga wake. Alaluya!

⁸⁶ Ngati iwo ankachita zimenezo nthawi imeneyo, mthunzi kumeneko, wa Mose akuyimba mu Mzimu; ndiye, uko mu Chivumbulutso, iwo amene ali ndi chiwombolo changwiwo cha thupi, anayima pa nyanja ya mandala ndipo anayimbanso nyimbo ya Mose, uko mu Bukhu la Chivumbulutso.

⁸⁷ Kukamba za a—msonkhano wa Mzimu Woyera? Iwo anakhala nawo iwo pamene anapita mmphepete mwa gombe limenelo. Mvetserani, mlongo. Miriamu wamng'ono wolemekezeka, mneneri wamkazi, mlongo wake wa Mose, mneneri wamkazi, iye anasangalala kwambiri mpaka anatenga nkhotcho ndipo anathamangira ku gombe, akumenya nkhotcho iyi, ndipo akuvina mu Mzimu. Osati izo zokha, koma ana aakazi onse a Israeli anamutsatira iye, akuvina mu Mzimu. Ngati uwo si Mzimu Woyera ukugwa, sindinayambe ndawuwonapo umodzi. Bwanji, ndithudi, iwo, mafuko onse amwambo, aulemu akanakhoza kuyang'ana kudzera pa magalasi owonera patali ndi kuwona izo, iwo akanakhoza kunena kuti, “Kutengeka.” Kulondola. Koma anali Mulungu. Kulondola!

⁸⁸ Zinthu zolemekezeka zimayang'anira pansu, lero, pa zomwe Mulungu wadalitsa. Kulondola!

⁸⁹ Zikundikumbutsa ine za nkhani. Munthu wina anali ndi munda waukulu wabwino kwambiri. Iye anamanga nkhekwe zabwino zazikulu, zolemekezeka ndipo zapamwamba momwe zikanakhallira, koma iye anali waulesi kulima. Chabwino. Kunali mlimi wina amene ankakhala pafupi ndi iye; iye analibe nkhekwe zambiri, koma anali mlimi weniweni, ndipo iye anali atayika zakudya zabwino zambiri mu nkhekwe imeneyo chaka chimenecho. Ndipo ana ang'ombe awiri anabadwa, mmodzi mu nkhekwe imodzi ndi wina mu inayo. Pamene nyengo ya masika inafika, iwo anawatulutsa ana a ng'ombewo mu khola.

⁹⁰ Mwana wa ng'ombe wamng'ono uyo wochokera kuno, anali atadyetsedwa bwino kwenikweni, mai, pamene mphelo imeneyo inayamba kumuwomba iye, oh, mai, iye anamenyetsa zidenede zake, ndipo anapita kutali, mwamphamvu basi momwe iye akanapitira; akulira, ndi kulumphu, ndi kumakuwa, ndi kumapitirira.

⁹¹ Ndipo kenako mlimi winayo anatulutsa wake, kumeneko. Iye anali—iye analibe kanthu koti adye koma udzu; waulesi kwambiri kuti alime, waulesi kuti amudyetse iye.

⁹² Zimandikumbutsa za ena a azibusa awa. Kulondola! Kulondola! Aulesi kwambiri! Ndi zochepa kwambiri. Ndipo nkhokwe zolemekezeka ndi zonse zimene inu muli nazo. Muyike Chakudya mmenemo cha mwana wa ng'ombe! Kulondola. Kulondola. Ubatizo wa Mzimu Woyera, wolalikidwa ndi mphamvu, udzawatentha iwo. Uko nkulondola. Koma icho ndi chimene iwo akusowa, ndi kutentha kwina kwachikale; chimene mpingo ukusowa, chimene mamembala akusowa. Zindikirani.

⁹³ Ndipo mwana wang'ombe wakale uyu anali atawonongedwa. Kanthu, kakang'ono kosauka kanatulukira mu khola, kanali kowonda kwambiri moti sikankakhoza kuyenda. Ndipo iye anasuzumira pansi pa mng'alu, ndipo anayang'ana kutsidya.

⁹⁴ Ndipo iye anawona mwana wang'ombe winayo akulira. Anali wonenepa komanso wozungulira. Iye anamva bwino. Iye anali akudya nyengo yonse yozizira.

⁹⁵ Ndipo mwana wang'ombe wamng'onoyo, wanjala uja anayang'ana uko, anati, "Kutengeka kotereko!" Mai! Ndithudi, anali wowonda kwambiri kuti aganize china chirichonse.

⁹⁶ Koma, ine ndikukuuzani inu, pamene mmodzi uyo amene ananenepa, nyengo yonse yachisanu, m'bale, iye amadziwa pamene iye anali. Iye anali akukhala ndi nthawi yabwino pamene mphepo yotenthayo inayamba kuwomba pa iye.

⁹⁷ Ndipo munthu aliyense amene abadwa mwa Mzimu wa Mulungu, iwo amamutcha iye wotengeka kapena china chirichonse. Koma pamene mphepo yotentha ija, ya masika, ya Mzimu Woyera iyamba kubwera monga Iyo inachitira pa Tsiku la Pentekoste, chinachake chidzachitika. Kulondola. Mphepo zofunda zimayamba kuwomba; m'bale, inu nonse mumanenepetsedwa ndi Uthenga, kuzungulira ndi kumamva bwino. Mumenyese zidendene zanu mmwamba ndi kukhala ndi nthawi yabwino.

⁹⁸ Umo ndi momwe Miriamu ndi iwo anachitira. Anayang'ana mmbuyo pansi ndipo anawona zinthu zonse zakale izo zomwe iwo poyamba ankazichita, zonse zinali zakufa ndipo zitapita. Iwo anali atamuwona Mulungu akuvomereza magazi; anali atawona kale mphamvu Yake mu machiritso Auzimu, itayima pakati pawo; anabwera kudutsa Nyanja Yofiira, ndipo anabatizidwa ndi Mzimu; anayenda mbali inayo, akungokhala ndi nthawi yabwino. Iwo sanasamale chimene... mabungwe onse ankaganiza za izo. Amen.

⁹⁹ Ndi choimira changwirowo bwanji lero, cha wokhulupirira amene angadzayesere kutuluka.

¹⁰⁰ Mulungu analonjeza kuti Iye adzapereka chosowa chawo chirichonse. Iye analonjeza kuti Iye adzapereka chosowa chathu chirichonse. Iye sanawauze konse iwo, "Ndipanga njira ya machiritso; Ndipanga njira ya *ichi*; ndipanga njira ya *icho*." Iye anati, "Ndidzakhala ndi inu!" Aleluya!

¹⁰¹ Ndicho chimene Iye ananena kwa ife. “Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumalekezero a dziko lapansi.” Ndizo zonse zimene ine ndikuyenera kunena. Inu simukuyenera kuti mutsutse *ichi, icho*, kapena *chinacho*. Ngati Iye ali pano, izo zikundikwanira ine; Machiritso Auzimu ali pano, Mphamvu ili pano. Chirichonse chimene Iye anali kumeneko, Iye ali pano, “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Chotero, inu mukhoza kutenga zaumulungu zanu ndi kumira nazo izo. M’bale, ine ndimakhulupirira Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse; anati, “Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumalekezero a dziko lapansi.” Inde.

¹⁰² Ndipo pamenepo iwo anatulukira, ndipo Iye anali ndi iwo. Tsopano iye anati . . . Oh, iwo anali ndi dengu laling’ono la mkate pa mitu yawo; iyo yonse inadyedwa ndipo inatha. Iwo analibe chirichonse. Iwo anapita kukagona, ali ndi njala pang’ono usiku umenewo. Koma mmawa wotsatira pamene iwo anazadzuka, mkate unali pansu paliponse.

¹⁰³ Umo ndi momwe Mulungu amachitira zinthu; amakulolani inu kuti mufike mpaka pa miniti yomaliza, kenako amakuwonetsani inu zimene Iye angathe kuchita za izo. Uko nkulondola. Iye amakonda kuchita zimenezo. Iye amakonda kutero. Iye amakonda kuwadabwitsa anthu Ake.

¹⁰⁴ Inu amuna mumakonda kumutero mkazi wanu. Mumadikira kufikira tsiku lake lobadwa, mumangomusiya iye azikaikira, chifukwa mumamukonda iye.

¹⁰⁵ Ndi chifukwa chake Mulungu amatilola ife kuti tizifika ku mapeto a msewu nthawizina, chifukwa Iye amatikonda ife ndipo amafuna kutsimikizira za chauzimu Chake ndi mphamvu Zake. Chifukwa Iye amatikonda ife, ndicho chifukwa Iye amachita zimenezo. Inde. Iye amangotilola ife kuti tifike pamalo amene ife tatsala pang’ono kupanga sitepe yotsiriza, kenako Iye amabwera pa chochitikacho.

¹⁰⁶ Iye anawalola ana a Chihebri kulowa mu ng’anjo ya moto, koma umo munali Munthu wachinayi atayima mmenemo ali ndi chokupizira, akutsekereza iyo kwa iwo. Mukuona? Iye nthawizonse amakhala pamenepo. Iye samachokapo nkomwe. Iye nthawizonse amakhala pafupi. “Mngelo wa Ambuye amawazinga iwo akumuwopa Iye.”

¹⁰⁷ Kumeneko, usiku umenewo, iwo anatola mkate umenewo mmawa wotsatira. Ine ndikukhoza kuwawona Aisraeli aja amene anali atangowoloka Nyanja Yofiira; anali atangowomboledwa kumene ndi magari; anawona Mphamvu yochiritsa ya Mulungu, kapena Mphamvu yozizwitsa itayima pakati pa Mulungu. . . ndi pakati pa Israeli ndi Igupto; ndipo anawamiza adani pambuyo pake.

108 Monga khansa yakale yapita kwanthawizonse, khungu linali litapita, kusamva kunali kutapita, matenda a shuga anali atapita, chirichonse chinali chitamizidwa uko mu Magazi a Yesu Khristu. Mukumverera bwanji? Mai!

109 Akuyenda chotsika mu msewu, ndipo wotsutsa wina wakale akuti, “Tsopano dikirani miniti! Kodi inu mukutsimikiza zimenezo?”

“Musayankhule ndi ine.” Ameni. Oh, mai!

110 Ine ndikutha kuwawona iwo kunja uko, akungosonkhana ndi kusunkhana, ndi kumadya, ndi kukhala ndi nthawi ya ulemelero. Chimodzimodzi monga ngati msonkhano wa kachitidwe-kachikale, wa Mzimu Woyera. Apa ukubwera Mzimu wa Mulungu ukudzasunthira kupita kwa woyera wina wamng’ono, ukufikira; ukudzafika mu mtima monga chomwecho, ndipo nkufuula, “Ambuye alemekezeke!” Msonkhano chabe wa kachitidwe-kachikale monga chomwecho. Inde, bwana. Iwo amangogwira izo kuchokera mbali imodzi kupita ku imzake, ankakhala ndi nthawi yabwino.

111 Tsopano, mkate umenewo sumatha konse. Iwo unayenda njira yonse kudutsa ulendowo, kwa iwo. Uko nkulondola. Ndipo chinali choyimira changwiro cha pentekoste mwa ife. Izo zinali mwathupi. Mkate umenewo sumatha konse. Iwo umakhalabe mkate womwewo, mpaka iwo anakalowa mdziko lolonjezedwa. Nkulondola uko? Inu owerenga Baibulo mukudziwa zimenezo. Ndipo kenako pamene ife . . .

112 Mpingo unatsegulidwa pa Tsiku la Pentekoste, pamene okhulupirira anali pamwamba uko. “Ndipo pamenezo panaturuka mkokomo ngati mphepo yamphamvu, inadzaza nyumba imene iwo anakhalamo.” Mzimu Woyera womwewo umene unagwa nthawi imeneyo, ukugwa tsopano. Iwo udzapitirira kuyambira nthawi imeneyo mpaka mapeto a nthawi. Iwo udzapitirirabe modutsa. Ndi mkate wathu. Iwo ankadyetsedwa ndi mkate wachirengedwe; ife tikudyetsedwa ndi mkate wauzimu.

113 Yesu anati, “Ine ndine Mkate wa Moyo umene umabwera kuchokera kwa Mulungu, kuchokera Kumwamba.”

114 Iwo anati, “Makolo athu ankadya manna mu chipululu, kwa danga la zaka forte.”

Iye anati, “Iwo ali, aliyenseyo, anafa.” Inde, bwana.

115 “Koma iye amene adya thupi Langa ndi kumwa Magazi Anga, ali nawo Moyo wosatha, ndipo Ine ndidzamuwukitsa iye mmasiku otsiriza. Ine ndine Mkate wa Moyo umene umachokera kwa Mulungu, kuchokera Kumwamba. Ngati munthu adya Mkate uwu, iye sadzafa konse.” Ndi zimenezotu. Iwo anali ndi chachirengedwe; ife tiri ndi chauzimu. Oh, ine sindingasinthanise icho ndi chirichonse. Zopambana!

116 “Oh,” inu mukuti, “M’bale Branham, ife tonse tikudziwa kuti ndinu wotengeka.” Chabwino, ine ndikutero, nanenso. Ndine chitsiru cha Khristu. Inu ndi chitsiru cha ndani? Inu mwina mukhoza kukhala chitsiru cha mdierekezi. Chabwino. Chotero, ine kulibwino ndikhale chitsiru cha Khristu, sichoncho inu? Chabwino.

117 Zindikirani, apa pali chinthu china cha manna amenewo. Pamene iwo anayamba kulawa iwo, iwo anati: “Iwo akukoma ngati uchi.” Inde, iwo anali okoma. Ine ndikutha kungowawona oyera akale amenewo akunyambita milomo yawo ndi kumadya. Iwo anali abwino.

118 Kodi inu munayamba mwalawapo *Izi? Izi* ndi zabwino, nazonso. Anati, “Lawani ndipo muwone, Ambuye ndi wabwino. Iwo akukoma ngati uchi mu thanthwe.” Nthawi zambiri ndapangapo ndemanga iyi, nthawi zambiri. Kuti, pamene Davide wakale, amene anayankhula zimenezo mu Salmo lake, anati, “Iwo akukoma ngati uchi mu thanthwe.”

119 Davide, pokhala m’busa, iye anali ndi kachikwama kakang’ono, iwo ankanyamula kumbali yawo, ndipo nthawizonse ankanyamula uchi mmenemo. Abusa akale amatero, komabe, mu—mu Palestina. Ndipo pamene zawo—nkhosa zawo zodwala zikamapitirira, ndiye, chinthu choyamba inu mukudziwa, iye amafikira pansi ndipo amapita kukatenga chidutswa chaching’ono cha uchi uwu, ndipo iye amautenga iwo ndi kuwupaka iwo pa thanthwe, thanthwe la laimu. Ndipo nkhosa zimakonda uchi umenewo, chotero iyo imanyambita uchi umenewo kuchokera pa thanthwe. Ndipo pali chinachake chokhudza miyala ya laimu chimene chimachiritisa nkhosa zodwala.

120 Ndipo ine ndikukuuzani inu, tiri ndi chikwama chodzaza uchi kuno usikuuno, ndipo tikawuyika iwo pa Thanthwe, Khristu Yesu. Ndipo nkhosa zodwala zikapita kumakanyambita, ndithudi inu mukhala bwino. Uko nkulondola, kumangonyambita, kunyambita, kunyambita. Ndipo pamene mukunyambita uchi, bwanji, inu mukhala otsimikizika kuti mudya laimu. Ndizo zotsimikizika basi monga chirichonse. Tsopano, ife sitiwuyika iwo pa mpingo. Ife tiwuyika iwo pa Khristu, kumene kuli kwawo. Uko nkulondola. Chifukwa, machiritso ali mwa Khristu, ameni, monga mdalitso wina uliwonse wa chiwombolo. Zindikirani.

121 Ndipo chinthu china. Pamene iwo anayamba kugwa, Aroni analamulidwa kuti apite ndi kukatenga ma omeri angapo ozadza a iwo.

122 Tsopano, ngati iwo ayesera kusunga ena kufika tsiku lachiwiri, iwo ankawonongeka. Ndipo izo ndi zochuluka kwambiri pakati pa anthu a Mzimu Woyera usikuuno. Inu mukuyesera kuganiza, “Chabwino, zaka twente zapitazo, ife

tinali ndi uthenga wabwino. Ife tinali ndi—tinali ndi nthawi yabwino.” Kodi muli ndi chiyani usikuuno? Ndicho chinthucho. Iwo . . .

¹²³ Iwo ankagwa usiku uliwonse. Iwo sanalepherepo nthawi imodzi, kokha pa—pa Sabata. Uko nkulondola. Ndipo tsopano Mulungu watumiza iwo pansi, atsopano, usiku uliwonse; tsiku lililonse, ora lililonse, iwo amabwera.

¹²⁴ Zindikirani, ma omeri amenewo ankasungidwa. Iye anati, “Tsopano, taonani, pamene inu mudzabwera mdzikolo, ndipo ana anu nkuyamba kufunsa za izi. . .” Anati, “Wansembe aliyense tsopano amene alowa mu unsembe, atatha kukhala ndi chilolezo chobwera ku malo Opatulika, ndi zina zotero, ndi kudzedwa, wansembe, ndiye iye akhala ndi ufulu wolowa ndi kudya manna odzaza kamwa apachiyambi amene ankagwa pachiyambi.” Oyamba enieni amene anagwa, iwo amawatola iwo ndipo amawayika iwo mu omeri, ndipo amawasunga iwo, ndipo amangungidwira unsembe.

¹²⁵ Tsopano inu mukuti, “M’bale Branham, kodi izo ziri ndi choyimira chotani lero?”

¹²⁶ Bwanji, ife ndi unsembe. “Inu ndinu unsembe wachifumu, fuko loyera, anthu achilendo, opereka nsembe zauzimu kwa Mulungu, zipatso za milomo yanu zikuyamika Dzina Lake.” Ameni. Ndi zimenezotu. Tsopano, ndiye, pa Tsiku la Pentekoste, pamene Mzimu Woyera unali kugwa; manna athu.

¹²⁷ Tsopano, wansembe aliyense kumbuyo uko, pansi pa Chipangano Chakale, pamene iwo ankabwera kuti adzakhale wansembe, iwo ankadziwa kuti azikadya manna apachiyambi odzaza mkamwa; osati ena ochita kupangidwa, ochita kupangidwa ndi anthu amene ankawoneka mofanana ndi iwo. Koma iwo anali oti azikadya ena apachiyambi.

¹²⁸ Chabwino, pa Tsiku la Pentekoste, pamene manna athu anayamba kugwa, Mzimu Woyera unabwera ngati mphepo yamkokomo yamphamvu. Apa panali gulu la anthu ochepa, aulemu, handiredi ndi twente, mchipinda chapamwamba; zitseko zitatsokedwa, mazenera atatsitsidwa, atakhala kumbuyo uko, akuyembekezera lonjezo. Eya, iwo anali ali ndi Yesu, ndithudi. Iwo ankadziwa mphamvu Yake, ndi zonsezo, koma iwo ankayembekezera lonjezo.

¹²⁹ Ndi zomwe tikufuna usikuuno. Kukhala. . . Ngati gulu la anthu ili likhoza kukhala la mtima umodzi, monga iwo anakhalira pa usiku umenewo, chinthu chomwecho chikhoza kubwerezedwa usikuuno, pomwe pano mchipinda chino, mu Louisville, Kentucky, chimene chinabwerezedwa pa Tsiku la Pentekoste. Uko nkulondola. Oh, ndithudi, iwo angadzakhale ndi mtundu womwewo wa otsutsa kuno mu Louisville amene iwo anali nawo kumeneko. Koma, iwo onse anali pa malo amodzi, a mtima umodzi. Ndipo mwadzidzidzi. . .

¹³⁰ Apo panabwera mtumiki, ndipo iye anali ndi kalata, ndipo iwo analemba maina awo ndipo anali ndi dzanja lamanja la chiyanjano, ndipo analowa mu chiyanjano cha mpingo? Izo zikhoza kukhala lero, koma izo sizinali nthawi imeneyo. Umo ndi momwe Achiprotectanti amachitira izo. Mkatolika amayenda kupita ku guwa ndi kutenga mgonero wake woyamba; amatulutsa lirime lake, amatenga kokulumunya; ndipo wansembe amamwa vinyo. Zikatero iye amadzakhala chimenecho.

¹³¹ Koma, m'bale, "Pa Tsiku la Pentekoste, iwo anali a mtima umodzi, pa malo amodzi, kenako mwadzidzidzi panamveka mkokomo kuchokera Kumwamba," munthu analibe chochita ndi Iwo, "monga mphepo yamkuntho wamphamvu. Iyo inadzadza nyumba yonse imene iwo anali atakhalamo." Mphamvu ya Mulungu inakantha pa iwo! Kunja mu msewu iwo anapita, akuchita ngati gulu la amisala; monga iwo anachitira kumusi uko pamene iwo ankadutsa Nyanja Yofiira. Nkulondola uko? Iwo anafuula. Iwo anapitirira. Iwo anadzandima. Iwo anachita chibwibwi ndi milomo yawo.

¹³² Iwo, oh, kupitirira koteroko, inu...mpaka anthu, mpingo wolemekezeka, anayima kumbuyo ndipo anati, "Anthu awa aledzera ndi vinyo watsopano.

¹³³ Aleluya! Munditcha ine "woyera wodzigudubuza," mulimonse, koteroko inu mukhoza kuyamba tsopano. Chabwino.

¹³⁴ Taonani, iwo anali odzazidwa ndi Vinyo watsopano, ndiko kulondola, Vinyo amene anachokera kwa Mulungu, kuchokera Kumwamba. Kodi inu munayamba mwamuwonapo munthu woledzera? Iye amangokhala mu chikondi ndi aliyense, inu mwaona. Iye samasamala. Umo ndi momwe munthu amakhalira pamene iye aledzera ndi Mzimu. Baibulo linati, "Musaledzere ndi chakumwa chaukali, mopitirira, koma kuledzera ndi Mzimu." Mzimu wa Mulungu umakuledzeretsa iwe kwambiri, iwe umaiwala adani ako onse, ndi chirichonse. Aliyense amakhala ali mu chikondi ndi iwe. Iye samasamala za amene wayima pafupi nawe. Iwe umakhala munthu wamkulu kwambiri mdziko pamenepo.

¹³⁵ Ine sindikusamala ngati woyandikana naye wanu, wakhala pafupi ndi inu, amapita ku mpingo wina wolemekezeka; mudzangolola Mzimu Woyera udzabwere pa inu nthawi imodzi, mudzawone zimene zimachitika. Mudzakhale bwino bwino, bwino kwenikweni, mudzaledzere kwambiri, mudzawona zimene zimachitika. Inu mudzati, "Mlongo, ine ndawupeza Iwo! Inu mukuufuna Iwo, inunso!" Uko nukulondola. Inde, bwana, chinachake chichitika.

¹³⁶ Apo iwo anali, onse ataledzera ndi Vinyo watsopano. Ndipo, mveterani, ena a inu alongo pano, kodi inu mumadziwa kuti namwali wodala Mariya anali mmenemo? Tsopano, iye anachita

kupita pamwamba kumeneko. Amayi a Yesu Khristu anachita kupita pamwamba kumeneko ndi kukaphatikizidwa mu gulu limenelo la anthu, analedzera kwambiri ndi Mzimu mpaka iye ankazandima ngati kuti waledzera ndi kachasu kapena chinachake.

¹³⁷ Ndipo inu mukuganiza kuti mudzapita Kumwamba pozembera kupita ku tchalitchi ndi kukayika buku lanu la nyimbo mkhwapa mwanu, ndi kumayenda mmawa wa Lamlungu lirilonse, ndipo belu likulira pang'onopang'ono, ndipo nkukhala ndi kumamvetsera kwa ena a...ndipo nkubwererako? Inu simudzachita konse zimenezo.

¹³⁸ Inu mukuyenera kudzera njira imeneyo, chifukwa ndiyo yokhayo imene Mulungu anayamba waiyikapo, ndipo yomwe ali nayo. Ndipo inu muziyenda mu imeneyo, kapena simudzakakhalako Kumeneko. Ine sindine woweruza wanu, koma ine ndikulalikira Uthenga. Ndizo ndendende Choonadi. Namwali wodalayo anali pomwepo, ankachita mopusa basi monga ena onsewo ankachitira, ataledzera basi monga ena onse a iwo. Amuna awa ndi akazi, aliyense wa iwo, anali odzazidwa ndi Vinyo watsopano. Ngati Mulungu anasinthapo dongosolo limenelo, muniyikire chala chanu pa Lembalo kwa ine; izo mulibemo mmenemo. Ayi, bwana. Izo zinali mpaka kumapeto kwa m'badwo, mwanjira imeneyo, mpaka ku mapeto a Baibulo, ndipo izo zidzakhala chinthu chomwecho pamene Yesu azidzabwera.

¹³⁹ Taonani! Pamene iwo anali chiledzerere ndi Vinyo watsopano ameneyo, taonani, ife tikuona ngati Mulungu anakuikirani inu nonse omeri wodzadza. Chabwino.

¹⁴⁰ Apa panali onse a iwo atayima kunjira uko, ndi mlaliki wamng'ono wamantha wachikulire dzina lake Petro, "mwala waung'ono," ankachita mantha kwambiri ndi udindo wake mpaka anamukana Yesu, ndipo anathamangira kunjira ndipo anapemphera mopitirira, ndipo iye ankayenera kusunkhana ndi iwo. Anayima pa nsanja yokwera kapena chinachake, anati, "Bwanji, inu amuna aku Yudeya, ndi inu okhala mu Yerusalemu!" Amenewo anali madokotala, D.D.'s. Oh, anati, "Inu amuna amene...ndi amuna a Israeli, ndi okhala mu Yerusalemu, ndi ena otero, mulole ichi chidziwike kwa inu. Awa sanaledzere, monga inu mukuganizira, popeza ndi ora lachitatu la tsiku. Koma ichi ndi chija..."

¹⁴¹ Ngati ichi si Chimenecho, ine ndikufuna kuti ndisunge ichi mpaka Icho chitadzabwera. Ndicho chinthu chimodzi.

¹⁴² Iye anati, "Ichi ndi chija chimene chinayankhulidwa ndi mneneri Yoweli, 'Izo zidzachitika mmasiku otsiriza, atero Mulungu, Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa mnofu wonse; ana anu amuna ndi aakazi adzanenera; ndi pa adzakazi Anga ndi antchito ndidzatsanulira Mzimu Wanga, ndipo iwo

adzanenera; ndipo Ine ndidzasonyeza zizindikiro mmiyamba, ndi pa dziko lapansi; ndi mizati yamoto, ndi utsi, ndi nthunzi; ndipo zidzachitika, lisanadze tsiku lalikulu ndi lowopsya la Ambuye, aliyense amene adzaitanira pa Dzina la Ambuye adzapulumutsidwa.”

¹⁴³ Gulu lija la omva-zawokha, ovala mwinjiro wautali, ansembe achinyengo, anati, “Kodi tingachite chiyani kuti tipulumutsidwe?”

¹⁴⁴ Petro anati, “Lapani, aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu ku chikhululukiro cha machimo anu, ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.” Nthawi yayitali bwanji? “Pakuti lonjezano liri kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa iwo amene ali kutali, ngakhale ochuluka amene Ambuye Mulungu wathu adzawaitana.”

¹⁴⁵ Ndiye, munthu aliyense amene walapa ndi kubatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, ndipo Mulungu wamupatsa iye ubatizo wa Mzimu Woyera, samapeza chinachake chowoneka ngati manna oyambirira, koma, iye samangotenga manna oyamba odzaza mkamwa okha, koma iye amapeza Mzimu Woyera womwewo wodzadza mumtima.

¹⁴⁶ Inu mutha kunena kuti, “Dulani izo pang’ono.” Ine ndikudziwa kuti ndikufuula pang’ono pa izo, koma basi sindingathe kudziletsa izo. Zindikirani, penyani. Ine sindikukukalipirani inu. Ine ndikhoza kukhala kuti ndikuphokosera nazo izo. Koma, oh, ngati inu mukanamverera monga ine ndinachitira, inu mukanafuula, nanunso.

¹⁴⁷ Zindikirani, oh, manna apachiyambi odzaza mtima amene ankagwa pachiyambi; Mzimu Woyera womwewo umene unagwa nthawi imeneyo, ukugwa tsopano. Ndipo kodi Iwo ungapite kuti? “Kwa inu, kwa ana anu, iwo amene ali kutali,” Louisville, Kentucky, “ndipo ochuluka amene Ambuye Mulungu wathu ati adzawayitane, adzalandira chinthu chomwecho chimene ife tiri nacho pano.”

¹⁴⁸ Ndicho chimene Iye ananena. Mulungu anadalitsa izo. Iye analalikira izo. Mzimu Woyera unawubweretsa Iwo; Ine ndinalandira Iwo; izo zikukhazikitsa izo. Ameni. Izo, izo nzabwino basi kwa ine. Ine ndinamutenga Iye pa Mawu Ake; Iye anachita izo. Ngati inu mukufuna Iwo, inu mukhoza kuwulandira Iwo, nanunso. Uko nkulondola.

¹⁴⁹ Chotero tulukani mu—chikhalidwe chakufa, ndipo mudzuke, ndi kungokugwedezeni inu monga choncho ndi kukudzutsani inu. Ndipo chinthu choyamba, muyang’ane pozungulira ndipo chirichonse chiziwoneka mosiyana kwa inu. Munthu ameneyo amene inu simukanati muyankhule naye, inu mudzafulumira kufika kwa iye ndipo mudzayankhulana naye; inde, bwana, mukungoyenera kuti muyankhule naye iye, ndizo zonse. Oh, zinthu zonsezo, kabwezeni zida zokonzera matayala zakale

zija uko, ndi zonse. . . zinthu izo zimene inu munazitulutsa mu hotelo nthawi imeneyo. Chopukutira chakale chiya chimene inu munachikulunga pa mbale za siliva zimene munazichotsa pa tebulo; inu mudzafulumira kubwerera, kuti mupite mukabweze icho. Inu ndithudi mudzatero. Inde, bwana. Izo zidzakupangani inu cholengedwa chatsopano mwa Khristu Yesu. Tsopano yang'anani pa Mariya. Oh, mai!

Tiyenera kuti tifulumire. Ife tikuyenda bwino.

¹⁵⁰ Apa iwo akupita, kudutsa mchipululu tsopano, utatha msonkhano wa kachitidwe-kachikale. Tsopano iwo ali pa ulendo wawo. Kodi si zachirendo kuti iwo anatsogozedwa molunjika kupita ku Chipululu cha Tchimo, mpaka ku chipululu, mpaka ku—kasupe wa madzi owawa? Kodi inu mungalingalire Mulungu akutenga ana Ake, iwo atangopulumutsidwa kumene ndi kudzazidwa ndi Mzimu Woyera, kupita ku kasupe a madzi owawa? Ndithudi. Iye akufuna kuwonetsera chikondi Chake kwa iwo kachiwiri. Uko nkulondola. Iwo anakafika kumeneko.

¹⁵¹ Inu mukudziwa, pamene inu mulandira Mzimu Woyera, inu mumakhala ndi zopinga zambiri. “Zochuluka ndi zosautsa za olungama, koma Mulungu amamupulumutsa iye kwa izo zonse.” Mulungu amakubweretsani inu, mukuyang'anizana nazo, kuti Iye akuwonetseni inu mphamvu Yake ndi ubwino Wake.

¹⁵² Monga ine ndinamva nkhani ya m'busa mu Yerusalemu, amene anathyola mwendo wa nkhosa yake. Iwo anati, “Bwanji, iwe m'busa wankhanza. Nchifukwa chiyani wathyola mwendo wa nkhosa?”

¹⁵³ Anati, “Chabwino, iyo simachita ngati imandikonda ine. Chotero ine ndinaganiza kuti ndingothyola mwendo wake, kuti ine ndithe kuyipatsa iyo chidwi china chapadera, ndipo ndikatero iyo izindikonda ine kuyambira pamenepo.”

¹⁵⁴ Nthawizina Mulungu amayenera kukugonekani inu chagada, ndi nthenda, imene adokotala amati inu mufa. Mulungu akhoza kukupatsani inu chisamaliro chapadera pang'ono kuti inu mumukonde Iye mochulukirapo. Uko nkulondola.

Ena kudutsa mmadzi, ena kudutsa mu
kusefukira,
Ena kudutsa mmayesero akuya, koma tonse
kudutsa Mmagazi;
Yesu amatsogolera Mpingo Wake.

¹⁵⁵ Tsopano, pamene iwo anali kumeneko, ndipo madzi anali akuwawa ndipo samatha kumwa, Mulungu anapereka njira. Mtengo waung'ono wakale ukugwedezeka pamenepo pa gombe, Mose anangowudula iwo ndipo anawuonyera iwo mmadzi, unasintha chinthu chonsecho; madzi abwino, okoma.

¹⁵⁶ Tsopano pamene inu mukumana ndi madzi anu owawa, kapena chinachake chimzake monga choncho, pali mtengo, usikuuno, kuyankhula mwauzimu, uli pa Gologota, kapena dziko, usikuuno, umene udzakometse madzi owawa aliwone amene mungatsogoleredwe nawo. Uko nkulondola. Kalvare adzakometsa chochitika chirichonse. Nthawi zambiri ife timafika mu malo ovuta, ndipo nkumadabwa bwanji. Chotero ine ndimatseka maso nthawizina, ndi kuganiza, “Kutali uko ku Gologota, kumene Muomboli wanga anakhetsa magari ndi kufera moyo wanga,” zitatero mlandu wanga unawoneka wawung’ono kwambiri. Ndimangoziponyera kumbali ndi kumayendabe. Izo zimapangitsa izo kukhala zokoma. Izo zimakometsa chondichitikira chirichonse chimene ine ndinakhalapo nacho. Iye nthawizonse amakometsa izo, pamene ndifika ku madzi anga a Marah.

¹⁵⁷ Tsopano, ife tiri pafupi kuwagwira iwo tsopano cha kuno mchipululu, zitatha zizindikiro zazikulu zonsezo ndi zodabwitsa. Chitsitsimutso chinali chitazilala. Ndipo chinthu choyambirira inu mukudziwa, pamene chitsitsimutso chinazilala, bwanji, iwo anayiwala zonse za zozizwitsa.

¹⁵⁸ Kodi zimenezo si chimodzimodzi basi zofanana ndi anthu lero? Iwo amayiwala zimene Mulungu anachita chaka chatha. Zimene Mulungu anachita pa msonkhano kunja kuno ku sukulu yapamwamba, inu munaiwala zonse za izo. Mukuona? Zimene Mulungu anachita, ife timangoiwala izo.

¹⁵⁹ Tsopano, zindikirani, ndipo chifukwa iwo amayamba kutsutsana wina ndi mzake, “Chabwino, ine kwenikweni, kuwonjezera apo, ndine wa Methodisti. Mpingo wathu ndi waukulu kwambiri.” “Ndine wa Baptisti, ndipo ine ndikuuzani inu pompano, ife timakhulupirira mu chitetezero Chamuyaya, ndipo ife tiri nacho Icho. Inu nonse mulibe chiphunzitso, kuwonjezera pamenepo.” Pamenepo ndi pamene inu mukhala mu vuto, ndipo madzi anu nkudulidwa. Uko nkulondola. Uko nkulondola.

¹⁶⁰ Pamenepo ndi pamene, chipululu, pamene iye amakhala kunja mu chipululu, amayamba kung’ung’udza, kung’ung’udza ndi kudandaula. “Chabwino, ine ndikuuzani inu. Ine ndikuuzani inu, pamene m’busa wakale uja anali kuno, mlaliki wakale uja amene ankalalikira chipembedzo chanthawi yakale monga choncho, ine—ine sindikudziwa ngati iye amalondola kapena ayi. Ine ndikukuuzani inu, iye—iye anawakwiwitsa amayi anga, usiku wina, iwo anapita kwawo. Ndipo ine ndikukuuzani inu, iwo anakondowezedwa, monga.” Iwo ankayenera kuti atero. Uko nkulondola. “Oh, ine sindikudziwa ngati ine ndikufuna kuti ndimve zochuluka za Izo, kapena ayi.” Ndipo apo ndi pamene madzi anu amadulidwa. Uko nkulondola. Ndi pamene inu mumafika mchipululu.

¹⁶¹ Iwo anayamba kung'ung'udza. Iwo anati, “Yathu—miyoyo yathu imanyansidwa ndi mkate wo pepuka uwu.” Iwo atasiya magaliki ndi anyezi za ku Igupto, ndipo anali akudya chakudya cha Angelo, ndipo nkumadandaulabe. Kodi zimenezo siziri monga mpingo? Tsopano ine ndikubwera kutsikira kwa anthu achiyero tsopano, inu nonse; eya, nonse a inu. Akudya chakudya cha Angelo, ndipo kenako anati, “Ine ndikanakonda tikanabwerera ku Igupto, kuti tikadye galiki wina.”

¹⁶² “Clayton McMichen ndi Wildcats yake akakhala ku bara kuja usikuuno. Ngati ine ndikanakhala kuti sindinajowine mpingo wakale umenewo, ine ndikanapita kumeneko.” Inu mukhoza kumapitirira. Kumene kuli chuma chanu, mtima wanu umakhala komwekonso. Inu munalibe kalikonse pamene inu munkayamba. Uko nkulondola. Uko nkulondola. “Oh, ine ndikufuna kuti ndichite *ichi*, kapena ndichite *icho*.” Ndi zimenezotu, nthawizonse kudandaula.

¹⁶³ Ndipo iwo anasiya madzi amatope a Igupto, kuti azikamwa madzi oyera ochokera mu Thanthwe la Mibadwo, ndipo amadandaula za Ilo. Iwo anasiya malo kumene asing'anga aakulu, odzitamandira a ku Igupto, odzitamandira aakulu ndi onse, kukakhala ndi Sing'anga Wamkulu. Iwo anachoka kumalo kumene iwo ankanena, kuti, “Masiku a zozizwitsa anapita,” kuti akakhale ndi anthu amene anali ndi zizindikiro ndi zodabwitsa zikuwatsatira iwo, ndipo komabe nkumadandaula. Oh, mai! Inde, bwana. Kumusi uko, ndithudi, Aigupto, iwo anali Amitundu ozizira, osayanjanitsika. Iwo sankakhulupirira mu chinthu choterocho ngati zozizwitsa.

¹⁶⁴ Kenako, iwo anali kunja kuno kumene iwo anali ndi Lawi la Moto litawazungulira iwo. Iye tiri nalo Ilo usikuuno. Iwo anali kunja uko kumene iwo anali ndi chisangalalo mu msasa, akufuula, zozizwitsa zikuchitika, ndi chirichonse, ndipo kenako nkumadandaula za izo. Nchifukwa chake madzi anadzauma, nchifukwa iwo analibe kanthu kotu adye kapena kumwa, chifukwa iwo ankang'ung'udza.

¹⁶⁵ Ndipo ndiro limene liri vuto ndi mipingo yozungulira Louisville, usikuuno; kung'ung'udza, kudandaula. Chifundo! Bwererani mu ntchito. Ndi zimenezotu.

¹⁶⁶ “Ndiye munthu uyu ndi ndani, Mose? Nchifukwa chiyani ife tinamvetsera, kumumvetsera mlaliki woyera wodzigudubuza uyu, mulimonse? Kodi ife tikuchita chiyani kunja kuno?” Ndipo madzi awo anaphwera.

¹⁶⁷ Ine ndikuganiza za Mose, munthu wamkulu uja. Iye anaphunzitsidwa mu nzeru—zonse za Aigupto. Tiyeni timuyang'ane iye kwa mphindi pang'ono chabe. Tiyeni timutenge Mose, kwa miniti yokha. Tayang'anani pa munthu ameneyo. Iye anali. . .

168 Aigupto, iwo anali kutali ndi ife lero, pamene izo zifika ku sayansi yathu ya zamankhwala. Iwo anali kutali ndi ife. Amatha kuchita zinthu zambiri zimene ife sitingathe kuzichita.

169 Ndipo Mose anali ndi mayankho onse. Ndipo pamene iye anali kunja uko, taganizani, Mose anali ndi pafupifupi anthu thu milioni ali ndi iye. Iye anali ndi ana aang'ono. Anali ndi amuna okalamba, akazi okalamba. Iye anali ndi olumala, ndi akhungu. Ana amabadwa, zikwizikwi za iwo, mu sabata. Ndipo Mose, Dokotala Mose, amakhala kunja uko mchipululu ndi anthu onse amenewa. Ine ndikufuna kuti ndiyang'ane mu chosungira mankhwala chake, simutero inu? Ine ndikufuna kuti ndiwone zimene Dokotala Mose anali nazo mu chosungira mankhwala. Tiyeni tingosuzumira pang'ono mosungira mankhwala ndipo tiwone zimene iye anali nazo.

170 “Mose, bwanji, kodi iwe unali ndi chiyani mmenemo, Mose?” Bwanji, ife tikupeza kuti mu ulendo wonse wa zaka forte umenewo, ana opitirira thu miliyoni anabadwa. Uko nkulondola. “Unkagwiritsa ntchito chiyani, Mose? Iwe unkagwiritsa ntchito chiyani pa zowawa zonsezo ndi kupweteka ndi khansa, ndi khungu, ndi kusamva, ndi kusayankhula? Bwanji, iwo amandiuza ine, kuti pamene inu munkatuluka mchipululu, panalibe mmodzi wofooka pakati pawo.” Ndikuti, kodi ena a madotolo awa sangakonde kuyang'ana mmenemo, kabati ya mankhwala imeneyo?

171 “Ndipo chinthu china, Mose, kodi iwe unkaonkha chiyani pa anthu amenewo, kufikira kuti zovala zawo sizimatha? Nsapato zawo sizimalala akuyenda pa miyala imeneyo.” Ngati inu munayamba mwapitako kumeneko, inu mukudziwa momwe chipululu chimawonekera, iwo amaimaliza nsapato mmasiku atatu. Ndipo iwo samatha nkomwe kuvala ngakhale chidutswa chimodzi cha chikopa pa iwo, mu zaka forte. “Mose, mosungira mankhwala mwako munali chiyani?”

172 Tiyeni tiyang'ane mmenemo. Ine ndikumuwona iye, “Ndiri ndi mankhwala amodzi, ‘Ine ndi Ambuye amene ndimakuchiritsani inu.’” Izo zikukhazikitsa izo. Amen.

173 Anati, “Oh, Mose, abambo anga akhala ali kuno, iwo angogwa ndipo athyola mwendo wawo. Iwe uli ndi chiyani cha iwo?”

174 “Ndiroleni ine ndiyang'ane ndi kuwona. ‘Ngati iwe udzamvera liwu Langa, kuchita zonse zimene ndikulamula, ine sindidzaika aliwonse a matenda awa pa inu, monga Aigupto, pakuti Ine ndi Ambuye amene ndimakuchizani inu.’ Ukawauze iwo zimenezo.” Iwo amachira. Amen. Uko nkulondola.

“Oh, iye wadwalika kwambiri! Mwana wanga ali ndi ntchirikilo, kapena chibayo, moyipa kwambiri! Dokotala Mose ine ndingapange chiyani?”

175 “Ndiroleni ine ndiwone chimene ine ndiri nacho. ‘Ine ndi Ambuye amene ndimakuchiritsani inu.’” Izo zimakhazikitsa zimenezo. Amen. Iwo amapita. Uko nkulondola. Kumapitirira, akusangalala. Ndizo zonse zimene iye ankasowekera, “Ine ndi Ambuye amene ndimakuchiritsani inu.”

176 Mwa sikisi handirede ndi chakuti, malonjezo otsimikizika a machiritso Auzimu, mu Chipangano Chatsopano chokha, ndipo komabe ife tikumukaikira Mulungu, usikuuno. Kodi Chiweruzocho chidzatanthauza chiyani kwa ife? Kulondola.

177 “Ine ndi Ambuye amene ndimakuchiritsani inu.” Inde, bwana. Ndicho chimene Mose anali nacho, Dokotala Mose anali nacho mmalo ake, mwake. . . mosungira mankhwala mwake, zinali ichi, “Ine ndi Ambuye amene ndimakuchiritsani inu.” Chotero Iye amachiritsa matenda onse, ndipo amawasunga iwo mwangwiro, ndipo anawabweretsa iwo kudutsa mchipululu, kupita ku dziko lolonjzedwa. Oh, mai!

178 Iwo anawasiya asing’anga aakulu onse awo, odzitukumula, kuti akakhale ndi Sing’anga Wamkulu uyu. Iwo anali atasiya gulu lija la anthu limene linali lozizira, lofunda, ndi losayanjanitsika, lakuti, “Kunalibe chinthu chonga ngati zozizwitsa.” Ndipo pomwe apa, Lawi la Moto linali litapachikika pa iwo. Anthu anali akuchiritsidwa. Chirichonse, ndi chinachonse chimene iwo ankachisowa, chinkangoperekedwa pomwepo kwa iwo, ndipo komabe iwo amadandaula pamene iwo anatuluka mmadzi. Komano mu chisomo cha pachokha cha Mulungu, mu zonsezo. . .

179 Monga inu muli kuno mu Louisville usikuuno, mkati mwa kulira konse uku, “Masiku a zozizwitsa anapita. Medical Association ikuyesetsa kuletsa machiritso Auzimu, kudutsa mdziko.” Inu simudzaletsa iwo konse. Inu mukhoza kungoletsa tsopano. Inu simungakhoze konse kuletsa izo kuposa momwe mungaimitsire dzuwa. Uko nkulondola.

180 Kuno zaka zingapo zapitazo, pamene ine ndinayamba koyamba mu Jeffersonville, ndinkalalikira machiritso Auzimu. Izo zinali zosadziwika, kwenikweni, kwa zaka. Ichu chinali chinthu chovuta. Koma, m’bale, usikuuno alipo mamilioni a iwo, konsekonse, akufuula. Kuyesetsa kuti ayimitse izo? Inu simungathe. “Ine Ambuye ndabzala izo; Ine ndidzathirira izo, usana ndi usiku, kuwopa kuti wina angandikhwatule izo mdzanja Langa.”

181 Kuno osati kale kwambiri, ine ndimayang’ana pa mpheta zina zazing’ono pa Statue of Liberty. Izo zinali zitangogona pamenepo. Zazing’onozo zinali zitagona mozungulira, pansu pa kuwala. Ndipo ine ndinati, “Chachita izo ndi chiyani?” kwa namulondola.

182 Iye anati, “Izo zinamenyetsa ubongo wawo, usiku watha, mu mkuntho umenewo. Izo zinalowa mu kuwalako, ndipo kuwalako

kukanatengera izo ku chitetezo, koma izo zimayesera kuti zidzimitse kuwalako. Ndipo izo zinamenyetsa ubongo wawo, poyesera kuti zidzimitse kuwalako.”

¹⁸³ Ine ndinati, “Ulemelero kwa Mulungu!” Ine ndikuganiza kuti iye amayesa kuti ndapenga. Ine ndinati, “Izo zikundiyyika ine mmalingaliro a ena a anthu awa akuyesetsa kuti agonjetse machiritso Auzimu ndi Mphamvu ya chiwukitsiro cha Yesu Khristu.” Inu mumenyetsera ubongo wanu kunj; inu simudzatero. Mungovomereza izo, ndipo muwulukire ku chitetezo, mmenemo. Uko nkulondola. Amen.

¹⁸⁴ “Muyankhule kwa thanthwe, Mose,” Mulungu anamuuzza Mose, “ndipo ilo lidzatulutsa madzi ake, lidzatulutsa madzi Ake.”

¹⁸⁵ Kuno osati kale kwambiri, ine ndinali kuyang’ana pa chithunzi mu nyumba yosungira zakale inayake, cha thanthwe ili likukanthidwa. Ndipo icho chinkawoneka ngati kamtsinje kakang’ono kakusefukira, pafupifupi kukula kwa singano yolukira. Ine ndinaganiza, “Ojambula awa angakhoze kukhala opusa bwanji!” Bwanji, m’bale, ine ndikhoza kumwa chinthu chimenecho mpaka kuuma ngati ine ndikanakhala ndi ludzu kumene. Inde, bwana.

¹⁸⁶ Kodi inu mukudziwa chimene Mose anali nacho kuti amwe kuchokera mu Thanthwe limenelo? Iye anali ndi anthu oposa thu miliyoni, pambali pa nyama zonse. Izo zinatengera pafupifupi zigubu forte sauzande pa miniti, kuti—kuti amwe, iwo. Aleluya!

¹⁸⁷ Izo zikundiyyika ine mu malingaliro a winawake mu chipembedzo chawo. Inu mwangokhala ndi chipembedzo chokwanira kupita ku Sande sukulu Lamlungu mmawa, kungolavula pang’ono ndi kukunyowetsani inu pang’ono.

¹⁸⁸ Ine ndimakonda kukhala pa Kasupe kumene mitsinje imatuluka, aleluya, yokwanira kunditengera ine kudutsa Muyaya. Aleluya! Ndine wokondwa kuti ndinachoka pa malo akale achinyezi amenewo; kupita ku chotsanulira kumene iwo amangotuluka nthawi zonse. Inde, bwana.

¹⁸⁹ Anthu angokhala ndi chipembedzo chokwanira kuti chiwapangitse iwo kukhala omvetsa chisoni. “Chabwino, ine sindingakhale kupitirira pafupifupi maminiti teni. Mai, kalanga, mlaliki ameneyo amatalikitsa motani?” Kodi chipulumutso chanu ndi chozama bwanji? Uko nkulondola.

¹⁹⁰ Kupita Lamlungu mmawa, ndipo nkumati, “Chabwino, ndipita uko ndi kukamva zomwe iwo ati akanene.” Ndipo nkukapeza chotsutsa chimodzi chaching’ono nkubwererako, ndipo ndizo basi zonse zimene inu muli nazo.

¹⁹¹ M’bale, ine ndikukuuzani inu, pamene Mose anakantha Thanthwe limenelo, ilo linathirira madzi chipululu chonse. Amen. Inde, bwana. Chinthu chokhacho, zonse zimene iwo

ankasowejera, iwo ankangogwera pansi pomwe ndi kumwa, kumwa, kumwa mpaka iwo ankangokhutitsidwa. Komabe, madzi ochuluka anali akutuluka, pafupifupi zigubu forte sauzande pa miniti. Talingalirani zimenezo, ndi anthu angati, anthu miliyoni, anthu thu miliyoni akhoza kumwa, mu miniti; anthu aludzu, pambali pa ngamila, ndi nyama, ndi zinthu zimene iwo anali nazo. Ndipo Baibulo linati, “Iwo anatuluka mochuluka.” Iye anangobangula, kudutsa mchipululu.

Umo ndi momwe Yesu Khristu amaperekera Mzimu Woyera.

¹⁹² Osati pang’ono chabe, kunena kuti, “Chabwino, ine ndikukhulupirira ine ndipita ndi kukajowina mpingo.” Oh, mai! “Oh, sindingathe kupirira phokoso limenelo. Ilo limandipangitsa ine manjenje.” Ngati inu mudzafike kumwamba, chifukwa, m’bale, inu mudzamva phokoso mukadzafika Kumeneko. Baibulo linati iwo amafuula “aleluya,” usana ndi usiku; tsiku lonse, chifukwa kulibe usiku. Uko nkulondola. Inu ndithudi mudzakafako mukadzakafika kumwamba, tsiku lachiwiri kumwamba Kumeneko. Inde, bwana. Chabwino, inu basi... chimene inu munachita, inu munangopita ndi kunyowa, pang’ono.

¹⁹³ Kodi simukhala pansi pafupi ndi madzi, ndi kuwasiya kuti atsike kufikira atakutsukani inu mu... aleluya, kupita pakati, ndipo kufikira inu mutadzitaya nokha ndipo osadziwa kumene inu muli. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Ndi mmene inu mukufuna kufikirako.

¹⁹⁴ Ine ndinkakonda kuwauza amalume anga, abambo anga, “Mnyamata, ine ndikhoza kusambira,” mu dziwe laling’ono ili kuno ku Utica Pike.

¹⁹⁵ Tsiku lina, abambo anabwerera ndipo anakakhala podutsa madzi, anati, “Ine ndikufuna ndikuwone ukusambira.” Dziwe laling’onolo linali lakuya pafupifupi *chonchi*. Ine ndinali nditaima pa ka nsanja. Ine ndinavula zovala zanga, ndipo ndinagwira mphuno yanga monga *chonchi*, ndipo ndinadumphira mmwamba-ndi-pansi mpaka pa ka nsanjako. Ine ndinadzagunda, matope anawulukira mbali zonse ziwiri, ndipo ndinayamba kukapiza matope.

Ine ndinati, “Ine ndikuchita bwanji, Adadi?”

¹⁹⁶ Anati, “Tuluka mmenemo.” Ukusambira? Ndimakwawa mmatope, nthawi zonse.

¹⁹⁷ Ife tiri ndi mamembala a mpingo ambiri okwawa mmatope, aponso. Uko nkulondola. Uko nkulondola, okwawa mmatope. Inde, bwana.

¹⁹⁸ Tsiku lina, amalume ananditengera mu bwato ndipo ine ndikapanga phokoso za kusambira; cha kuno mu Mtsinje wa Ohio, pafupifupi mapazi twente a madzi. Iwo anangotenga nkhamu ndipo anandikankhira ine mmadzi, anati, “Tsopano

nanga bwanji zimenezo?” Ameni. Aleluya! Ine ndinkayenera kuti ndisambire kapena kumira, ndiye. Oh, mai!

¹⁹⁹ Mwinamwake mukhoza kuzolowera Izo tsopano. Kukupititsani inu mu kasupe, mmene Mulungu akutsegula thanthwe mchipululu ndipo nkungotsanulira ilo. “Yankhula kwa Thanthwe,” Iye anatero, “ndipo ilo litulutsa madzi Ake.”

²⁰⁰ Mwinamwake, mzanga, usikuuno, mwinamwake iwe ukuwonongeka. Iwe ukuyenera kuyankhula kwa Thanthwe. Uko nkulondola.

²⁰¹ Mwinamwake iwe wapitapo kulikonse. Mwinamwake iwe unapitapo ku tchalitchi, ndipo unajowinapo Methodisti, ndipo nkudzajowina Baptisti; ndipo iwo anakukwiwira iwe, ndipo unapita ku Presbateria; ndipo unabwerera kwa Achipentekoste, uko ku Nazarene, mpaka ku Pilgrim Holiness. Ndipo iwe ukadali wopanda kumvetsa.

²⁰² Iwe uingoyankhula kwa Thanthwe, usikuuno. Basi...Kodi iwe uli moyankhulana ndi Iye? Eya. Iye anati, “Yankhula kwa Thanthwe, ndipo Iye adzatulutsa madzi Ake.” Ilo lidzatulutsa madzi Ake, ngati inu munga...Simukuyenera kuti mumumenye Iye, aponso. Mungoyankhula ndi Iye. Basi pa kumvana kwa ubwenzi, yankhulani ndi Iye.

²⁰³ Mwinamwake mwapitako kwa adokotala. Mwinamwake mwapanga chirichonse chimene mumadziwa kuchichita kwake, kuti muyesere kuti mukhale bwino. Mwinamwake mwangochita chirichonse chimene chiri mu mphamvu yanu, pafupifupi, ndipo simukupeza bwino. Dokotala aliyense, mwadutsa mu ofesi iliyonse imene inu mumaidziwa, ndipo adokotala anati, “Inu basi...Palibe chomwe chingachitike kwa inu.” Bwanji inu osayankhula kwa Thanthwe, usikuuno? Iye adzatero...Iye ali ndi madzi a Moyo kumeneko a inu, kukupatsani inu Moyo wochulukwa kwambiri.

²⁰⁴ Nthawi ina kunali mkazi, mu Baibulo, dzina lake Hagara. Ine ndikuganiza za iye. Ndipo ine ndikukonzekera zoti nditseke; nthawi. Kunali mkazi dzina lake Hagara, ndipo iye anali ndi mwana wamng’ono. Iye anathamangitsidwira kupita mchipululu, ali ndi botolo limodzi laling’ono la madzi. Iye ankamudyetsa mwana wamng’ono, tsiku lonse. Koma madziwo anatha, cha pakati pa tsiku, ndipo mwana wamng’ono ankakuwa ndi kumalira. Milomo yake yaing’ono inali youma ndipo lirime lake linkatupa. Mayi wosauka, wokonedwa, iye akanachita chiyani? Iye anali atafufuza malo aang’ono aliwonse amene iye akanatha, kuti apeze madzi, koma madzi sanapezeke. Iye sakanapirira kuti awone mwanayo akufa; chotero iye anamuyika iye pansu pa tchire, ndipo anapita kamtunda pang’ono.

²⁰⁵ Ndipo iye anagwada pansu ndipo anayankhula kwa Thanthwe. Pamene iye anayankhula kwa Thanthwe, Mngelo

anayankha ndipo anati, “Hagara, chikutuluka apocho ndi chiyani?”

²⁰⁶ Apo panali chitsime chonse, chodzaza ndi madzi, chimene chikuyendabe lero. Zitatha zaka pafupifupi foro sauzande, icho chikugwirabe ntchito lero. Kasupe amene Hagara . . . pamenepo, ameneyo, akuyendabe lero. Iye anayankhula kwa Thanthwe, ndipo Thanthwe linabweretsa madzi.

²⁰⁷ Panali ana ena Achihebri analowa mu ng’anjo yamoto, tsiku lina, ndipo iwo anayankhula kwa Thanthwe. Ndipo Thanthwelo linali ndi iwo.

²⁰⁸ Panali mkazi amene anabwera kuchokera ku Samaria, nthawi ina. Iye anakhumudwitsidwa. Iye anali wochimwa, ndipo anali ndi zinthu zambiri zikulendewera pa moyo wake, mwinamwake. Ndipo anakhumudwitsidwa. Iye anapita ku chitsime cha Yakobo kuti akapeze thandizo, ndipo amabwerera. Iye ankapita ku chitsime cha Yakobo, ndi kubwererako. Ndipo tsiku lina iye anayika mtsuko wa madzi pansi, ndipo anali atayima pamenepo, atakhumudwa. Ndipo pamenepo panali Thanthwe, litaima pafupi ndi iye. Iye anayankhula kwa Thanthwe limenelo. Iye anamupatsa iye kasupe wamkulu mmoyo wake. Iye anathamangira mu mzinda. Iye sanabwerenso kudzatunga, kenanso. Iye anapeza Moyo. Iye anati, “Bwerani, mudzawone Mwamuna amene wandiuza ine chirichonse chimene ine ndinachita. Kodi uyu si Khristu?” Iye anayankhula kwa Thanthwe, ndipo Thanthwe linatulutsa madzi Ake.

²⁰⁹ Panali mkazi wina wamng’ono amene anawononga ndalama zake zonse kwa madokotala, onyengezera, amene ankatenga ndalama zake zonse. Samatha kuyimitsa vuto la magazi. Iye mwinamwake anali atabwereketsa munda wake, ndipo mwinamwake anawugulitsa iwo. Ndipo iye anali atakhala, akuluka tsiku lina, ndipo iye anamva Chinachake chikubwera pansi pa msewu. Iye anayankhula kwa Thanthwe. Thanthwelo linatembenuka ndipo linati, “Ndani wandikhudza Ine?” Izo zinatha pamene iye anayankhula kwa Thanthwelo. Iye anamupatsa iye kasupe wa Moyo, amene anayimitsa vuto la magazi. Ilo linasiya, mwamsanga.

²¹⁰ Kunali wopemphetsa wachikulire wakhungu atayima pambali pa khoma, tsiku lina, akunjemera mu kuzizira. Zonse zimene iye anali nazo zinali zitapita. Ndipo apa iye anali, ndipo womvetsa chisoni, ndipo anthu akumudutsa. Iye anamva Chinachake chikubwera; anati, “Icho ndi chiyani?” Ndipo iye anayankhula kwa Thanthwe.

²¹¹ Ngakhale, mamembala a mpingo wake, omuzungulira iye, anayesera mukuletsa iye, kuti, “Palibe chofunikira. Iwe sungapeze izo. Khala kutali. Khala chete.”

²¹² Koma iye anafuula mokweza, “Inu mwana wa Davide, ndichitireni ine chifundo! Ndichitireni ine chifundo!” Ndipo iye

anayankhula kwa Thanthwe, ndipo Thanthwe linamupatsa iye kasupe, ndipo maso ake anatseguka.

²¹³ Thanthwe lomwelo limene linali mchipululu liri pano lero. Ilo limawakondweretsa anthu.

²¹⁴ Tsiku lina, Yerusalemu yense anali atayima kuti awone mchiritsi Wauzimu, woyera wodzigudubuza, akulowa mu mzinda; ndi anthu apang'ono atayima pamenepo, akufuula pamwamba pa mawu awo, "Hosanna! Hosanna, kwa Iye amene akubwera mu Dzina la Ambuye!"

²¹⁵ Mamembala odzimva-okha aja a mpingo anali kunja uko atavala miinjiro yawo yaitali, ndi ma D.D awo kumbuyo kwawo; anati, "Aloleni iwo akhale chete. Mai, iwo amapangitsa kuti tsemwe liziyenderera pa nsana wanga, ndi zina zotero. Kuwapangitsa iwo kukhala chete."

²¹⁶ Iye anati, "Ngati iwo akhala chete, miyala idzalira nthawi yomweyo." Nchifukwa chiyani izo chomwecho? Thanthwe lomwelo limene linadulidwa kuchokera mu phiri, popanda manja, linali likubwera, likugudubuzikira mu Yerusalemu. Matanthwe aang'onowo anali akumwa kuchokera kwa Ilo. "Yankhulani kwa thanthwe, ndipo Ilo lidzatulutsa madzi Ake."

²¹⁷ Ngati inu mukufuna chipulumutso, usikuuno, yankhulani kwa Thanthwe. Ilo litulutsa madzi Ake. Ngati ndinu wobwerera mmbuyo, usikuuno; yankhulani kwa Thanthwe, Ilo litulutsa madzi Ake. Ngati inu muli pano, usikuuno, ndipo opanda Khristu; inu mwayesera mpingo uliwonse umene ulipo, mu mzinda, kuti mupeze chipulumutso; yankhulani kwa Thanthwe, Ilo lidzatulutsa madzi Ake. Inu mukukhulupirira zimenezo? Ngati ndinu wobwerera mmbuyo, munachoka kwa Mulungu, mukuganiza kuti palibe mwayi kwa inu; ingoyankhulani kwa Thanthwe, ndipo Ilo lidzatulutsa madzi Ake.

²¹⁸ Kodi inu mukukhulupirira zimenezo, ndi mtima wanu wonse? Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu angapereke izo? Ndi mtima wanu wonse, inu mukukhulupirira izo? Aleluya! Iye ali pano usikuuno.

²¹⁹ Ngati inu mukudwala, ndipo mwayesera chirichonse mdziko. Inu mwayesera kuti mulowe mu mzere wa pemphero, ndipo inu simungathe kulowa mu mzere wa pemphero. Inu mwakhalapo ndi makadi apemphero, ndipo mwakanidwa. Mwapitapo ku msonkhano umodzi; inu munapita ku msonkhano wina. Inu munadzozedwapo ndi abusa. Inu mwadutsa mu mzere wa pemphero uwu. Inu mwakhala kwina kulikonseko, ndipo mukulephera kuchiritsidwa.

²²⁰ Bwanji osayankhula kwa Thanthwe tsopano? Iye adzatulutsa madzi Ake. Uko nkulondola. Bwanji osamuyesa Iye kamodzi? Mufike pomayankhulana ndi Iye, pakali pano, pamene Iye ali mchipinda chino. Kukhalapo Kwake kuli pomwe pano tsopano kuti achize aliyense wa inu. Ine ndikukhulupirira

zimenezo. Ine ndikudziwa izo, ndi mtima wanga wonse. Ine ndikukhulupirira. Ndipo pali zinthu zina zimene ine sindikuzidziwa, koma pali zinthu zina zimene ine ndimazidziwa. Ndipo ine ndikudziwa kuti Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo, ali pompano.

²²¹ Pamene ine ndikuyesera ngakhale kuti ndiitanire ku guwa pakali pano, mu mtima mwanga, masomphenya akusweka ponse ponse mchipindamu—pompano. Oh, uko nkulondola. Mphamvu za Mulungu ziri pomwe pano. Uko nkulondola. Ine ndamuwona Iye akuyenda kunja kuno. Iwo ayamba kundipititsa ine kuchoka ku dera lina kupita ku lina, pakali pano; chifukwa pali anthu odwala pano, ndipo mapemphero anu ndi amene akuchita zimenezo; kuti atsimikizire Mawu a Mulungu, kunena kuti Iye ali pomwe pano kuti tiyankhule naye, usikuuno, Thanthwe lomwelo limene linayima ndi kuzindikira maganizo awo. Anawona kumene mkaziyo anali, yemwe anali ndi vuto la magari, ndi zina zotero. Iye ali pano tsopano. Ngati inu mungayankhule kwa Iye, Iye adzatulutsa madzi Ake. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo ndi mtima wanu wonse?

²²² Inu mukuganiza chiyani, dona? Ndi. . . Pomwe apo pakati. Tsopano, inu mulibe khadi la pemphero, sichoncho inu? Dona amene ali ndi chinthu choyera mozungulira khosi lake, wakhala pomwe apo. Muli ndi nthenda ya shuga, sichoncho inu? Inu mulibe khadi la pemphero, sichoncho inu? Inu simukusowa khadi la pemphero lirilonse. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Kodi inu mukuganiza kuti mukhoza kuyankhula kwa Thanthwe? Kodi inu mukufuna kuti muyankhule ndi Iye, za matenda anu a shuga, pakali pano? Imirirani pa mapazi anu ndiye. Nkulondola uko? Mungonena kuti, “Ndikumuvomereza Yesu Khristu tsopano ngati mchiritsi wanga,” ndipo Mulungu akutengerani kwanu ndipo akakuchiritsani inu. Yankhula kwa Thanthwe. Mulungu akudalitseni. Chabwino. Pitani, ndipo mukachiritsidwe.

²²³ Kodi inu mukuganiza chiyani za izo, mwakhala pafupi ndi iye, dona? Inu muli ndi mitsempha yotupa mmiyendo yanu, sichoncho inu? Uko nkulondola. Imirirani pa mapazi anu. Uyo si mwamuna wanu wakhala pafupi ndi inu pamenepo? Nkulondola uko? Inu muli ndi nthenda ya shuga, nanunso, sichoncho inu? Nkulondola uko? Ikani dzanja lanu pa mkazi wanu. Chabwino. Nonse awiri mukuchokera ku Illinois. Si kulondola uko? Tsopano inu muzibwerera ku Illinois, mukuyankhula kwa Thanthwe, ndipo iyo ikusiyani inu ndipo siidzabwereranso kachiwiri. Aleluya!

²²⁴ Ine ndikudziwa chinthu chimodzi, kuti Thanthwe liri pano, Thanthwe la Mibadwo limene linakanthidwa mchipululu. Uko nkulondola.

225 Kodi inu mukuganiza chiyani za izo, dona wamng'ono apo muli ndi maluwa awo pa chipewa chanu? Mwakhala pamenepo ndi nyamakazi, mukuyesera kuti muthane nayo iyo. Inu amene munatembenuka ndi kuyang'ana mbali ina, kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse kuti Mulungu akuchizani inu? Imirirani pa mapazi anu ndiye, ndipo mupondetse mapazi anu mmwamba-ndi-pansi, ndi kuti, "Nyamakazi yapita," ndipo izo ziri choncho. Yankhulani kwa Thanthwe, ndipo Iye adzawatulutsa...?...

226 Ine ndikukuuzani inu, Yesu Khristu yemweyo, dzulo, lero, ndi kwanthwazonse. Iye ali pano kuti awonetsere chirichonse chimene...

227 Inu mukuganiza chiyani za izo, dona wakhala apoyo, anati, "Ambuye alemekezeke," ndi vuto la chikazi limenelo, wavala jekete laling'ono, lowoneka lagirini, wakhala apoyo? Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu wakuchiritsani inu ndiye? Imirirani, miniti chabe; mwakhala pomwe apo. Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Muli ndi vuto la chikazi. Ndi chotupa. Muli ndi njira, ngalande ya mtundu wina ikuchokera mmenemo. Si kulondola uko? Ngati izo ziri zolondola, kwezani dzanja lanu. Nchiyani chikundipangitsa ine kunena zimenezo? Ndi Thanthwe limene likuyankhula kwa inu. Yankhulaninso kwa Iye, ndipo muchiritsidwe. Aleluya!

228 Oh, momwe Iye akufunira kubweretsa mawonetseredwe Ake a mphamvu Yake! Ndipo ine ndikumuwona Mngelo wa Mulungu, Lawi la Moto lomwelo limene linkawatsatira ana mchipululu, likusuntha kudutsa mchipinda chino tsopano.

229 Ine ndikuyesera kuti ndimupeze mkaziyo. Iye akupemphera. Kodi ali kuti pano? Apa Iye waimirira. Inde, ndi mkazi wamng'ono wayima pomwe apo, wachiwiri wakhalayo. Ayi, iye...Ndi zokhudza mwamuna, wayima. Ndi mwamuna woledzera amene mukumupempherera. Kodi si kulondola uko, dona? Ngati ndi choncho, imirirani pa mapazi anu pomwepo. Kodi inu mulibe mwamuna woledzera amene mumamupempherera? Ngati izo ziri zoono, kwezani mmwamba dzanja lanu. Yankhulani kwa Thanthwe, ndipo Mulungu amutulutsa iye mu—mu chinthucho.

230 Mulungu achita chirichonse mkati muno, ngati inu mungachite izo. Kodi inu mukukhulupirira izo? Kodi inu mukumayankhulana naye Iye? Ngati ndi inuyo, imirirani pa mapazi anu pakali pano ndipo muyankhule kwa Thanthwelo, ndipo Thanthwelo, litulutsa madzi Ake. Kodi inu mungaimirire?


231 Ndani akumufunira Iye chipulumutso? Kwezani dzanja lanu, nenani, "Ine ndikumufuna Iye kuti abwere mu mtima mwanga." Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, ndi inu, ndi inu, ndi inu. Oh, mai! Inde, bwana.

²³² Khansa ija yakusiyani inu pamenepo, m'bale wanga. Iyo yapita. Inu mukhoza kupita kwanu ndi kukakhala bwino tsopano. Aleluya! Izo nzoona.

²³³ Onse amene akufuna kuti achiritsidwe, kwezani dzanja lanu, nenani, “Ambuye, ine ndikuyankhula ndi Inu. Ine ndikuyankhula ndi Inu.” Uko nkulondola.

²³⁴ Apo iye akupita. Bambo, chimfine chanu chakusiyani inu pamenepo. Ndinu mfulu. Pitani kwanu; mu Dzina la Yesu Khristu, inu mwachiritsidwa.

²³⁵ Aliyense muno, amene akufuna kuti amupeze Iye tsopano, kwezani mmwamba manja anu ndi kunena, “Zikomo Inu, Ambuye, pondichiritsa ine. Ine ndikuyankhula ndi Inu, mu Dzina la Yesu Khristu, kuti Inu mundichiritse ine.”

²³⁶ O Mulungu, wachifundo, tumizani mphamvu Yanu usikuuno, ndi kudzoza kwa Mzimu Woyera, pamene Iye ali mchipinda chino tsopano, kuti asese pa omvetsera awa. Ndipo mulole Mzimu Woyera uchite chozizwitsa chirichonse. Mulole pasakhale wodwala kapena munthu wolumala atatsale mchipinda chino usikuuno. Inu muchiritse aliyense, mu Dzina la Yesu Khristu. 

CHIWOBOLO KUKHALA CHOTSIRIZIKA, MU CHISANGALALO CHA54-0330
(Redemption In Completeness, In Joy)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lachiwiri madzulo, Marichi 30, 1954, ku Church Of The Open Door mu Louisville, Kentucky, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2023 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org